KHULĀSAH NŪR AL-YAQĪN MCHICHEWA

Lolembedwa ndi:

Umar Abd al-Jabbār (r.a)

Ndipo latanthauziridwa mchichewa ndi:

Zaid Bunāya Abū Muhammad

(Allah amuyang'anire nthawi zonse, Amin)

(1) CHAKA CHOYAMBA PAMBUYO PA NSAMUKO

Kumangidwa kwa Masjid yolemekezeka - Chiyambi cha Adhān - Adhān ya Fajr mmwezi wa Ramaḏān - Adhān ya Jumu`ah

(1) Mchaka choyamba pambuyo pa nsamuko, Mtumiki (s.a.w) adamanga Masjid yake yolomekezeka. Ndipo ndithu Iye mwini adagwira nawo ntchitoyi, kuti awalimbikitse Asilamu kugwira ntchito (molimbika).

(2) Ndipo mchaka chomwechi idakhazikitsidwa *Adhān*[1]*;* kuti idziwazindikiritsa ozengereza ndi kuwakumbutsa oyiwala, ndikuti kusonkhana kudzikhala kwakulu.

(3) Ndipo Bilāl (r.a) adawonjezera mu *Adhān* ya Fajr mawu akuti: "***Mapemphero ndi abwino zedi kuposa kugona***", kawiri. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adagwirizano nazo zimenezi.

4. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adali kulamura za (kuchita) ma *Adhān* awiri pa Fajr ya mmwezi wa *Ramaḏān*; yoyamba yodzutsa nayo omwe sakudziwa (chifukwa chakugona) kuti adzuke ndi kudya daku, ndipo yachiwiri ya mapemphero.

5. Ndipo *Adhān* ya Jumu`ah idali imodzi yokha kuchokera nthawi ya Mtumiki (s.a.w) mpakana utsogoleri wa *Abūbakr* ndi *`Umar* (r.a); yomwe inkayamba pamene *Imām* wakhala pa mimbar (pa tsanja), ndipo inkachitikira pa khomo la Masjid.

6. Ndipo *`Uthmān* (r.a) adaonjezera *Adhān* yachiwiri[2], chifukwa cha kuchuluka kwa anthu.

---

[1] Mtumiki (s.a.w) adawafunsa maganizo ma Saḥābah ake kuti adzichita bwanji pamene nthawi yopemphera yakwana. Chomwecho ena mwa Iwo adati: "Tidzinyamula mbendera". Ndipo ena adati: "Tidziyatsa moto pamwamba pa zulu", pomwe ena adapereka maganizo a chitoliro monga momwe amachitira Ayuda, ndipo ena adati koma (tidziimba) beru monga momwe amachitira Akhirisitu, ndipo ena adapereka maganizo a muyitano (mkuwo). Chomwecho Mtumiki (s.a.w) sadagwirizane nawo maganizo onsewa koma ganizo lotsirizirali, ndipo mmodzi mwa ochita muitano (umenewu) adali `Abdullah mwana wa Zaid (r.a). Chomwecho tsiku lina Iye ali mtulo adamuonekera munthu wina ndikumuphunzitsa Adhān. Choncho pamene adadzuka adamufotokozera Mtumiki (s.a.w) za maloto amenewa, choncho Mtumiki (s.a.w) adati: "Ndithu awa ndi malotho owonadi". Ndipo adamulamura kuti amuphunzitse Bilāl (r.a). Ndipo pamene `Umar adaimva (Adhanayo) adati: "Ndikulumbira Allah, (nane) ndidalota zofanana ndi zimenezi".

[2] Pamene *Hishām* mwana wa *`Abdul-Malik* adatenga utsogoleri (wa Asilamu) adaichita Adhanayi (kuti idzichitiikira) pamaso pa ochita Khutbah (*Khaṯīb*), chomwecho chimenechi ndi chinthu chopekedwa chomwe chilibe tanthauzo lililonse; kamba kakuti Adhān ndi muitano (oitanira) ku mapemphero, ndipo munthu yemwe ali kunja kwa Masjid sangaimve Adhān imenei.

MAFUNSO

Kodi ndi chaka chanji chomwe Mtumiki (s.a.w) adamanga Masjid yake? Kodi *adhān* idakhazikitsidwa chaka chanji? Kodi Bilāl (r.a) adawonjezera chiani mu adhān ya Fajr? Kodi Mtumiki (s.a.w) adali kulamura chiani pa Fajr ya mu Ramadān? Kodi adhān ya Jumu`ah idali motani? Kodi ndani yemwe adaonjezera adhān yachiwiri.

(2) AYUDA AKUMADĪNAH

Udani wawo ndi Chisilamu – Kufotokoza kwawo za Mtumiki asadatumizidwe – Amunafiqūn a ku Madīnah – Pangano ndi Ayuda

1. Pamene Ayuda a ku *Madīnah* adaona kufalikira kwa Chisilamu mmenemo, adawonetsera chidani pa Asilamu ndipo adayamba kulimbikira pa kuwabweza ku Chisilamu.

2. Ndipo Iwo kale adali kuwafotokozera ma Arabu a ku Madīnah za mneneri amene adzatumizidwa yemwe nthawi yake ili pafupi, chomwecho pamene Iye adatumizidwa, atsogoleri awo adachiona kukula zedi kuti mneneriyo akhale ochokera mwa ma Arabu[3].

3. Ndipo linali kuwathandizira pa ntchito yawoyi gulu lina la Amunafiqūn (anthu achinyengo) mwa ma Arabu a ku Madīnah, omwe amatsogoleredwa ndi *`Abdullah* mwana wa *Ubayy* mwana wa *Salūl*.

4. Chomwecho pamene Mtumiki (s.a.w) adaona zimenezi kwa iwo, adakhazikitsa nawo pangano pa fundo zakuti; asamusawutse ndikuti nayenso asawathire nkhondo, ndikutinso asalimbane ndi chipembedzo chawo. Tsono akakhala Amunafiqūn Iye anali kulandira kwa Iwo zomwe zikuwonekera pamwamba ndikusiya zomwe zabisika (mwa iwo)[4].

MAFUNSO

Kodi adachita chiani Ayuda ataona kufalikira kwa Chisilamu ku *Madīnah*? Kodi anali kuwafotokozera chiani Aluya a ku *Madīnah* kale? Ndani omwe anali kuwathandizira pa ntchito yawoyi? Kodi nchiani chomwe adachita nawo Mtumiki (s.a.w)?

---

[3] Umboni wake ndi mau ake (Allāh) wapamwamba-mwamba (onena kuti): "***Ndipo pamene buku lidawadzera lochokera kwa Allāh, loikira umboni pa zomwe zili limodzi ndi Iwo (adalikana) pomwe kale (lisadadze bukulo), adali kupempha chithandizo kupyolera mwa Mtumiki olonjezedwa, chongojetsera amene sadakhulupirire. Koma pamene chidawadzera chimene amachidziwa (Qur'ān) adachikana. Chomwecho matemberero a Allāh ali pa osakhulupirira***".

[4] Amunafiqūn amenewa anali ngati chilonda (cha mphutsi) pa thupi la Asilamu, koma kuti Allāh adamukwanira Mtumiki (s.a.w) pomuteteza ku zoipa zawo, ndipo adawulula (ndikuyalutsa) zinsinsi zawo ndi ndale zawo, ndipo adamuchenjeza Mtumiki (s.a.w) kuti asawadalire. Ndipo umboni wa zimenezi ndi mau ake Iye Wapamwamba-mwamba (onena kuti): "***Ndipo ena mwa anthu amchipululu omwe akukhala mphepete mwanu alipo Amunafiqūn (achinyengo), ndiponso eni mzinda wa Madīnah, aphunzira ukatswiri wa chinyengo (kotero kuti sukuwadziwa, Ife tikuwadziwa***".

(3) KUMENYANA (NKHONDO)

Kuloleza za kumenya (nkhondo) – Chiyambi chake – Chiwerengero cha nkhondo zing'ono-zing'ono – Chiwerengero cha nkhondo zikulu-zikulu – Cholinga cha kuika miyala pa mitumbila ya manda

1. Allāh adawaloleza[5] Asilamu kumenyana nawo adani awo pambuyo pa kulimbana kwawo ndi Mtumiki (s.a.w) ndikupereka masawutso kwawo pa Iye, ndikugwirizana kwawo za kumupha Iye.

2. Chomwecho kudayambika kumenyana (nkhondo) mchaka choyamba ndi gulu laling'ono la nkhondo (*Sariyyah*)[6] lomwe adalitumiza Mtumiki (s.a.w) motsogoleledwa ndi bamboo ake akulu *Hamzah* (r.a), kuti akatchingire mdipiti wa ngamira (zonyamula katundu)[7] wa maquraysh omwe umabwerera kuchokera ku *Shām* (Syria). Ndipo kenako adatsatizana magulu a nkhondo zing'ono zing'ono ndi nkhondo zikulu-zikulu.

3. Ndipo chiwerengero cha nkhondo zake zing'ono zing'ono chidafika 77, pomwe chiwerengero cha nkhondo zake zikulu-zikulu (chidafika) 27.

4. Ndipo adamwalira mchaka choyambachi *`Uthmān* mwana wa *Madh`ūn* (r.a), m'bale wake wa Mtumiki (s.a.w) pa kuyamwila bele limodzi.

5. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adalamura za kuwaza madzi pa thumbira (la manda ake), ndipo kenako adayika mwala pamwamba pake ndipo adati[8]:

---

[5] Allāh adawaloleza ma Muhājirūn (Asilamu osamuka) kumenyana ndi Amushrikīn achiquraysh pambuyo pakuti adawatulutsa mdziko lawo popanda chilungamo, ndipo umboni wa zimenezi ndi mau ake Wapamwamba-mwambayo (akuti): "***Chaperekedwa chilolezo kwa Asilamu amene akuputidwa (ndi adani awo kuti abwezere), chifukwa chakuti Iwo achitiridwa zoipa. Ndipo ndithu Allah Ngokhoza kuwathandiza. Omwe atulutsidwa mnyumba zawo popanda chilungamo, koma pachifukwa chakuti akunena; "Mbuye wathu ndi Allāh***". Komanso mau ake Iye Wapamwamba-mwambayo (onena kuti): "***Ndipo menyani nkhondo pa njira ya Allāh (modziteteza) ndi amene akukuthirani nkhondo, koma musalumphe malire, chifukwa chakuti Allāh sakonda olumpha malire. Ndipo apheni paliponse pomwe mwawapeza ndipo atulutseni paliponse pamene adakutulutsani, chifukwa kusokoneza anthu pa chipembedzo chawo nkoipa zedi kuposa kupha. Koma musamenyane nawo pafupi ndi Msikiti oyera pokhapokha atayamba ndiwo kukumenyani pamenepo. Chomwecho ngati atamenyana nanu pamenepo, inunso menyananawoni. Motero ndi momwe ilili mphoto ya osakhulupirira***.

[6] *Sariyyah* (سَرِيَّةٌ) ndi nkhondo iliyonse yomwe Mtumiki (s.a.w) sadakhale nawo Iye mwini, pamene *ghazwah* (غَزْوَةٌ) ndi nkhondo iliyonse imene anakhala nawo limodzi Mtumiki (s.a.w).

[7] *`Īr* (عِيْرٌ) ndi gulu la ngamira zomwe zanyamula katundu osiyana-siyana (monga chakudya ngati matumba a tirigu ndi zina).

[8] Ichi ndicho cholinga choyikira miyala pa manda osati zomwe amalinga anthu anthawi zathu zino zomwe ndi zoletsedwa pa Sharī`ah, ndipo zatsimikizika (mmahadith) kuti Mtumiki (s.a.w) adamulamura `Ali (r.a) kuti asasiye thumbira lililonse la manda lonyamuka koma alifafanize pa nthaka, ndi fano lililonse koma aliphwanye-phwanye. Ndipo Imām Al-Shāfī` (r.a) adafotokoza m'buku la Al-Umm kuti: "*Ndikukonda kuti pasawonjezeredwe pa manda dothi lina*".

"***Ndikuika ichi ngati chizindikiro cha manda a m'bale wangayu, ndipo ndidziwayika motere omwe amwalira mwa akubanja langa***".

MAFUNSO

Kodi ndi chaka chanji chomwe Allāh adawaloleza Asilamu kumenyana ndi adani awo? Kodi kumenyana kudayamba ndi chiani? Tchulani chiwerengero cha nkhondo zake zing'ono zing'ono? Ndani yemwe adamwalira mchaka choyamba? Nanga nchiani chomwe adalamura pambuyo pa kumuika mmanda?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHOYAMBA

Mchaka choyamba Mtumiki (s.a.w) adamanga msikiti wake, ndipo mchaka chomwecho *Adhān* idakhazikitsidwa. Ndipo mchaka chomwechonso Ayuda a kumadīnah adawonetsera udani pa Asilamu, ndipo adawathandizira (pa zimenezo) Amunāfiqūn (anthu achinyengo) a kumadīnah, chomwecho Mtumiki (s.a.w) adakhazikitsa (pangano) pakati pake ndi pakati pawo. Ndipo mchaka chomwecho adatumiza bamboo ake akulu ndi gulu laling'ono la nkhondo kuti likatchingire gulu la ngamira la maqurayash lonyamula katundu. Ndipo kenako zidatsatizana nkhondo zikulu-zikulu ndi nkhondo zing'ono-zing'ono, mpakana chidafika chiwerengero cha nkhondo zing'ono zing'onozo pa **47** ndi nkhondo zikulu-zikuluzo pa **27**. Ndipo mchaka chomwecho adamwalira m'bale wake wa Mtumiki (s.a.w) oyamwila naye bele limodzi, chomwecho adalamura za kuwaza madzi pa manda ake pambuyo pa kumuika, ndipo kenako adaika mwala pamwamba pake ndipo adati: "***Ndikuika ichi ngati chizindikiro cha manda a m'bale wanga***".

4. CHAKA CHACHIWIRI PAMBUYO PA NSAMUKO

Nkhondo zake: Nkhondo ya Qaynuqā`

1. Mchaka chachiwiri idachitika nkhondo ya *Waddān*[9] ndi *Buwāṭ*[10] ndi *Al-`Ushayrah*[11] ndi *Badr* yoyamba[12] ndi *Qarqaratul-Kadr*[13], ndipo simudachitike monsemo kumenyana kulikonse. Ndipo mchaka chomwecho mudachitika nkhondo ya *Badr* yaikulu ndi *Qaynuqā`* ndi *Al-Sawīq*[14].

2. Ndipo *Qaynuqā`*[15] ndi mtundu wa anthu a ku Madīnah omwe adawonetsera udani pa Asilamu, ndipo adachita chinyengo (pakuswa) zomwe adalonjezana naye Mtumiki (s.a.w).

---

[9] *Waddān* ndi mudzi omwe uli pakati pa Makkah ndi Madīnah. Adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita kumeneko limodzi ndi anthu makumi asanu ndi limodzi (60) kuti akatchingire gulu la ngamira lonyamula katundu la maquraysh, koma sadalipeze.

[10] Limeneli ndi phiri mbali za ku Yanbu`, adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita kumeneko limodzi ndi asikali apazokwera okwana zana limodzi (100) kukatchingira gulu la katundu, koma sadalipeze.

[11] Limeneli ndi dambo (khwawa) lomwe lili pafupi ndi Yanbu`. Adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita kumeneko limodzi ndi asikali apazokwera okwana mazana awiri ndi makumi asanu ndi limodzi (250) kukatchingira gulu la ngamira lonyamula katundu.

[12] Amenewa ndi madzi omwe ali pakati pa Makkah ndi Madinah. Ndipo imatchedwanso kuti nkhondo ya *Safwān*.

[13] Malo ena pafupi ndi ku Madīnah

[14] Sawīq ndi ufa wabwino kapena wapamwamba zedi wa tirigu mkulu-mkulu (*wheat/ḥinṭah*) kapena tirigu wamg'ono-mng'ono (*barley/sha`īr*). Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita ku nkhondo imenei ali limodzi ndi asikali apazokwera okwana 200, chomwecho pamene Amushrikuna adamva za kubwera kwake adathawa. Ndipo panthawiyo anali ndi phala lomwe anali kulitaya uku akuthawa pofuna kupeputsa katundu wawo, chomwecho nkhondoyi idatchedwa kuti *Sawīq*, kutanthauza "phala".

[15] Mtumiki adawuthira nkhondo mtundu wa *Banī Qaynuqā`* pambuyo pa nkhondo ya Badr yaikulu, chifukwa chakuti Iwo adaphwanya zomwe adapangana naye Mtumiki (s.a.w). Adawononga ulemu wa mkazi wina olemekezeka mwa ma Ansār, chomwecho Allāh adavumbulutsa (mau awa): "***Ngati uwopa kusakhulupirika kwa anthu (omwe unapangana nawo chipangano), atayire chipangano chawocho mwachilungamo. Ndithu Allāh sakonda anthu osakhulupirika***". Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawasonkhanitsa atsogoleri awo ndikuwachenjeza mathero oipa a kuchita chinyengo, koma Iwo adayankha mayankhidwe oipa, chomwecho Allāh adavumbulutsa (mau awa): "***Awuze omwe sadakhulupirire (kuti); "Posachedwapa mungonjetsedwa ndikusonkhanitsidwa ndikuponyedwa ku moto wa Jahannam. Taonani kuipa kwa malo okhazikika. Ndithudi padapezeka chisonyezo chachikulu kwa inu mmagulu awiri omwe adakumana (tsiku la nkhondo ya Badr), pomwe gulu limodzi limamenya (nkhondo) pa njira ya Allāh, pomwe linalo lokanira linkwawona Asilamu kukhala ochuluka kawiri kuposa ilo, powona ndi maso awo. Ndipo Allāh amalimbikitsa mphamvu ndi chipulumutso chake amane wamufuna. Ndithudi mzimenezo muli malingaliro (akulu) kwa eni kupenyetsetsa mwanzeru***". Ndipo ena mwa achinyengo adawonetsera ubwezi kwa Ayuda, ndipo mtsogeleri wawo *Abdullah* mwana *Ubayy* mwana wa *Salūl* adati: "Ine ndi munthu amene ndikuopa tsoka". Chomwecho Allāh adabvumbulutsa (mawu awa); "***E! Inu amene mwakhulupirira! Ayuda ndi Akhirisitu musawapale ubwenzi (nkumawauza chinsinsi chanu). Iwo pakati pawo ndi abwenzi ndi atetezi kwa wina ndi nzake. Amene awapale ubwenzi mwa inu ndiye kuti Iye ndi mmodzi wa Iwo. Ndithudi Allāh satsogolera anthu ochita zoipa. Uwawona omwe mmitima mwawo muli matenda (achinyengo) akuthamangira kwa Iwo (Ayuda) uku akuti: "Tikuopa lingatigwere tsoka". Koma***

3. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawazungulira (ndi gulu la nkhondo) masiku khumi and asanu (15), mpakana adawafowoketsa ndikulowetsa mantha mmitima mwawo.

4. Chomwecho adamupempha Iye kuti awasiye ndikutenga chuma chawo. Chomwecho Iye adavomera (zimenezo) kwa iwo ndipo adawapilikitsa ku Madīnah limodzi ndi akazi awo, ndipo Asilamu adatenga chuma chawo ndi malinga awo. Ndipo sipanadutse chaka koma onse mwa iwo adamwalira (ndikutha psiti).

MAFUNSO

Kodi ndi ziti nkhondo zomwe zidachitika mchaka chachiwiri? Kodi *Qaynuqā`* ndi ndani? Kodi adachita nawo chiani Mtumiki (s.a.w)? Kodi Iwo adapempha chiani kwa Iye?

posachedwapa Allāh abweretsa lamulo longonjetsa (midzi) kapena chinthu china chochokera kwa Iye, choncho adzasanduka odzinena chifukwa cha zomwe adabisa mmitima mwawo".

5. NKHONDO YA *BADR* YAIKULU

1. Nkhondo ya Badr yaikulu ndiyo cholekanitsa (pakati pa chowona ndi bodza) yomwe Allāh adapereka nayo ulemelero ku Chisilamu, ndikunyamula kuwala kwake, ndikuzimitsa Shirk, ndikuziwononga nsichi zake.

2. Ndipo choyambitsa chake nchakuti Mtumiki (s.a.w) adatuluka kuti akatchingire mdipiti wa ngamira[16] zonyamula katundu wa maquraysh, omwe umabwerera kuchokera ku *Shām*, ndipo adali limodzi ndi anthu mazana atatu ndi khumi ndi atatu (313).

3. Chomwecho pamene adadziwa maquraysh za zimenezi, adatumiza anthu mazana asanu ndi anai ndi makumi asanu (950) kuti akateteze mdipiti wawo ndi malonda awo, chomwecho Mtumiki (s.a.w) adayenda kupita kwa iwo[17] limodzi ndi omwe adali naye, ndipo adamenyana nawo kumenyana kwa mphamvu.

4. Ndipo Allah adawathandizira Asilamu ndi angero, choncho Amushrikunaa adagonja kuthawa, ndipo Asilamu adawalondola uku akuwapha ndi kuwagwira.

5. Chomwecho anaphedwa mwa Amushrikuna anthu 70; mmodzi wa iwo anali *Abū Jahl*, ndiponso anagwidwa akapolo makumi asanu ndi awiri (70). Ndipo anaphedwa mwa Asilamu anthu khumi ndi anai basi (14).

---

[16] Mtsogoleri wa mdipiti umeneu adali *Abū Sufyān* mwana wa *Harb*, chomwecho pamene adamva za kutuluka kwa Mtumiki (s.a.w), adatumiza mthenga kwa maquraysh kuti akawafotokozere zimenezi.

[17] Mtumiki (s.a.w) adawafunsa maganizo ophunzira ake asadawuyambe ulendo kuti kodi achite zotani. Chomwecho *Sa`d* adati: "Ndithu Ife tidakukhulupirirani ndi kukuvomerezani ndipo tidaikira umboni kuti zomwe mwabwera nazo ndizo zoonadi, ndipo tidakupatsani pa zimenezo malonjezo ndi mapangano athu pakukumverani ndi kukugonjerani. Chomwecho pitirizani chomwe mwachifunacho pakuti Ife tonse tili nanu limodzi. Ndipo tikulumbirira Allah! Ngati inu mukadatibweretsa pamaso pa nyanja iyi ndikulowa nafe mmenemo ife tikaidalowa nanu limodzi; ndipo sakadatsalira mmbuyo aliyense wa ife, ndipo sitikuopa kukumana ndi adani mawa lino". Ndipo *Al-Miqdād* adanena kwa Iye kuti: "Pitani chitsogolo E! Inu mthenga wa Allah monga momwe Allah wakulamulirani, pakuti ife tili nanu limodzi. Tikulumbira Allah, ife sitinena monga adanenera ana a Izrayeli kwa Musa (s.a.w) kuti: "Choncho pita Iwe ndi Mbuye wako ndi kumenyana nawo, Ife tikhala pompano". Koma tinena kuti: "Choncho pita Iwe ndi Mbuye wako ndi kumenyana nawo, Ife tili nanu limodzi kumenya nkhondo". Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adasangalala ndi yankho lawo ndipo adayenda nalo gulu la nkhondo mpaka adafika pa nthaka yamchenga ndi mchere yopanda madzi. Chomwecho Asilamu adali ndi ludzu ndipo ena adali ndi Janābah (litsiro lalikulu lofunika kusamba), ndipo ena adali ndi litsilo laling'ono, chomwecho Allah adawatsitsira mvula yomwe makhwawa adayenderera chifukwa chake, chomwecho adamwa ndi kuchita Wudū ndikusamba, ndipo adapanga timadamu ndikusungamo madziwo. Ndipo nayonso nthaka idalimba ndi kugwirana bwino kotero kuti mapazi adalimbangana poyenda. Pomwe akakhala Amushrikuna ndiye mvula idachititsa matope pa nthaka yawo kotero kuti samakwanitsa kunyamuka. Ndipo umboni wa zimenezi ndi mau ake (Allah onena kuti): "**Ndipo anavumbwitsa mvula pa Inu yochokera ku mitambo kuti akuyeretseni nayo (matupi anu) ndikukuchotserani nayo manong'on-nong'o a Satana, ndikuipatsa mphamvu mitima yanu ndiponso kulimbitsa mapazi anu pamchenga**".

6. Ndipo kenako adalamura Mtumiki (s.a.w) za kuika (mmanda) mitembo ya Asilamu ndi Amushrin, ndipo anabwerera ku Madinah. Ndipo pamene adaiyandikira adamuchingamira Iye adzakazi (atsikana) ndi ting'oma (maduf) uku akuyamba (kuti);

"**Watulukira kwa Ife mwezi owala**", …….mpaka kumapeto.

MAFUNSO

Kodi nkhondo ya Badr yaikulu ndi chiani? Kodi choyambitsa cha nkhondoyi nchiani? Kodi maquraysh adachita chiani atadziwa zimenezo? Kodi Allah adawalimbikitsa ndi chiani Asilamu pa nkhondo imenei? Tchulani chiwerengero cha ophedwa mwa Asilamu ndi Amushrikin pa nkhondo imenei? Kodi Mtumiki (s.a.w) adalamura chiani pambuyo pake?

6. MWATUMIZIDWA NDI CHOWONADI NDI CHILUNGAMO

1. Adaimirira Mtumiki (s.a.w) pa nkhondo ya Badr ndi ndodo mmanja mwake, chomwecho adamudutsa *Sawād* mwana *Ghaziyyah* (r.a) uku Iye atatuluka munzere. Choncho adamumenya ndi ndodoyo pa mimba pake, ndipo adati kwa Iye; "Ima bwino E, Iwe *Sawād*!". Chomwecho Iye adati: "Mwandipweteka inu Mtumiki, chikhalirecho inu mwatumizidwa ndi chowonadi ndi chilungamo, choncho ndiloleni pa inu mwini kuti ndikubwezereni". Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adavundukula mimba yake ndipo adati: "Bwezera Iwe Sawād!". Chomwecho *Sawād* adamukumbatira Iye ndikupsyopsyona mimba yake.

Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati: "Nchiani chomwe chakupangitsa zimenezi?". Iye adati: "Ndidafuna kuti chinthu changa chomalizira chikhale chakuti khungu langa likhudzane ndi khungu lanu". Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamupemphera zabwino.

KUWOMBOLEDWA KWA AKAYIDI A NKHONDO YA BADR

2. Adafunsa maganizo Mtumiki (s.a.w) ophunzira ake pa zomwe angachite ndi akapolo a nkhondo ya Badr, chomwecho `Umar (r.a) adamulangiza Iye za kuwapha, pomwe Abubakr (r.a) adamulangiza Iye za kuwasiya (amoyo) ndikutenga dipo kwa iwo kuti likhale (chopereka) mphamvu kwa Asilamu pa Amushrikin.

3. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adagwirizana nawo maganizo a Abubakr (r.a) ndipo adalamura kuti asamasulidwe aliyense (mwa akaidiwo) koma kupyolera mu kulipiria dipo basi, ndipo (dipoli) linali kuyambira ndalama za golide zikwi zinai (4,000) mpakana chikwi chimodzi (1,000).

4. Koma akakhala osawuka ndiye kuti yemwe amakwanitsa kulemba ndi kuwerenga mwa iwo, Mtumiki (s.a.w) amamupatsa khumi (10) mwa ana a ku Madinah kuti awaphunzitse (kulemba ndi kuwerenga), ndipo zimenezo zinali dipo lake.

MAFUNSO

Fotokozani chidule cha zomwe zinachitika pakati pa Sawād ndi Mtumiki (s.a.w)? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani ndi akapolo ogwidwa pa Badr? Kodi ndi maganizo ati omwe adagwirizana nawo Mtumiki (s.a.w)? Kodi osawuka adadzimasula ndi dipo lanji?

(7) MALAMURO OKHAZIKITSIDWA

Kutembenuzidwa kwa Qiblah – Kusala kwa mmwezi wa Ramaḏān – Zakāt ya Fitr – Zakāt ya chuma

1. Mchaka chachiwiri kuchokera mu nsamuko idatembenuzidwa Qiblah kuchokera ku *Baytil-Maqdis* (Yerusalemu) kupita ku Ka`bah, pambuyo pakuti adapitirira Asilamu kulunjika ku *Baytil-Maqdis* kwa miyezi khumi ndi isanu ndi umodzi (16).

2. Ndipo mmwezi wa *Sha`bān* Allah adakakamiza kusala kwa mmwezi wa *Ramaḏān* pa Asilamu; kuti osala alawe kuwawa kwa njala ndi ludzu, chomwecho mtima wake ufewe ndipo makhalidwe ake asinthike, kotero kuti kukhale kofewa kwa iye kupereka zopereka za ulele.

3. Ndipo mmwezi omwewo adakakamiza Allah *Zakāt* ya *Fitr* (chopereka cha kumaliza kusala), chifukwa cha kuwamvera chisoni amphawi ndi osawuka ndi ofowoka, komanso pofuna kukwaniritsa zosawukira zawo ndi kufuna kulowetsa chimwemwe mwawo iwo.

4. Ndipo momwemonso Allah adakakamiza *Zakāt* ya chuma (chosiyana-siyana) ndi kuipereka ku mitundu isanu ndi itatu (ya anthu osowa), ndicholinga chakuti chipitirire chikondi pakati pa olemera ndi amphawi, potero adzithandizana ndi kupulumutsana, (ndikuti) chitetezo ndi bata zikhale mmalo mwake.

5. Ndipo momwemonso adakhazikitsidwa mapemphero awiri a idi, ndicholinga chakuti akwanitse ana (anthu) a mzinda umodzi kusonkhana (ndikubwera malo amodzi) mmasiku awiri a idi ya *Fitr* ndi idi ya *Ad-hā*.

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe idatembenuzidwa Qiblah kuyang'ana ku Ka`bah? Kodi ndi liti lomwe Sawm idakakamizidwa? Ndi liti lomwe idakakamizidwa Zakat ya Fitr? Ndi liti lomwe idakakamizidwa Zakat ya chuma? Ndi liti lomwe idakakhazikitsidwa Salah ya ma idi awiri?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHACHIWIRI

Mchaka chachiwiri idachitika nkhondo ya *Waddān* ndi *Buwāṭ* ndi *`Ushayrah* ndi *Badr* yoyambilira ndi *Qarqaratil-Kadr*, ndipo monsemo munalibe kumenyana kulikonse. Ndipo momwemo idachitika nkhondo ya Badr yayikulu; pamene Mtumiki adatuluka kuti akatchingire mdipiti wa ngamira wa maquraysh ndipo adali naye limodzi anthu mazana atatu ndi khumi limodzi kudza atatu (313).

Pamene maquraysh adadziwa za kutuluka kwake adatumiza anthu mazana asanu ndi anai ndi makumi asanu (950). Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamenyana nawo mpaka anagonja kuthawa. Ndipo anaphedwa mwa iwo makumi asanu ndi awiri (70) ndipo anagwidwa ukayidi anthu makumi asanu ndi awiri (70). Ndipo sanaphedwe mwa Asilamu koma anthu khumi ndi anai basi (14).

Ndipo adakakamiza Mtumiki (s.a.w) dipo (lodzimasulira) kwa olemera chomwecho maquraysh adawaperekera dipole. Koma akakhala osawuka (mwa iwo) ndiye dipo lawo (lodzimasulira) lidali kuphunzitsa ana aku Madinah kuwerenga ndi kulemba.

Ndipo mchaka chomwechi idachitika nkhondo ya Bani Qaynuqa`, (omwe ndi mtundu ochokera mwa Ayuda a ku Madinah omwe adaswa pangano) – chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawazungulira ndipo adawapilikitsa ku Madinah.

Ndipo mmenemo idatembenuzidwa Qiblah; kuchokera ku Baytil Maqdis kupita ku Ka`bah, ndipo kudakakamizidwa kusala kwa (mwezi wa) Ramadan ndi Zakat ya Fitr ndi Zakat ya chuma, ndipo idakhazikitsidwa Salah ya ma Idi awiri.

Ndipo adakwatirana Ali ndi Fatimah zaka zake zili makumi awiri ndi chimodzi (21) ndipo Iye (Fatimah) ali ndi zaka khumi ndi zisanu (15). Ndipo momwemo adalowana Mtumiki (s.a.w) ndi Aishah zaka zake zili zisanu ndi zinai (9).

Ndipo mchaka chimenechi adamwalira Ruqayyah (r.a) mwana wa Mtumiki (s.a.w).

(8) CHAKA CHACHITATU CHA NSAMUKO

Nkhondo zake – Nkhani ya Da`thūr ndi kulandira kwake Chisilamu

1. Mchaka chachitatu idachitika nkhondo ya *Ghaṭfān* ndi *Bahrān*, ndi nkhondo ya *Uhud* ndi *Hamrā' al-Asad*, ndipo mudalibe kumenyana kupatula nkhondo ya *Uhud* (yokha basi).

NKHONDO YA *GHATFĀN*

1. Adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita ku nkhondo ya *Ghatfān* kukamenyana ndi ma Arabu omwe amafuna kuchita chiwembu Madinah.

2. Chomwecho pamene adamva za kutuluka kwa Mtumiki (s.a.w), adathawira ku songa za mapiri chifukwa cha kuwaopa Asilamu.

3. Ndipo zidachitika kuti Mtumiki (s.a.w) adavula chovala chake kuti achiwumitse (chomwe chidanyowa) chifukwa cha mvula yomwe idachinyowetsa, ndipo adapumula pansi pa mtengo uku Asilamu atamwazikana.

4. Chomwe adamuona Iye mu Arabu wina dzina lake *Da`thūr*, choncho adabwera kwa Iye ndi lupanga lake mpakana adaima kumutu kwake ndipo anati: "Ndani angakuteteze kwa Ine E! Iwe Muhammad?". Chomwecho Mtumiki adati: "Allah!". Chomwecho munthuyo idamufika nthumazi ndi mantha choncho lidagwa lupanga mmanja mwake, ndipo adalitenga Mtumiki (s.a.w) nati: "Ndani angakuteteze kwa Ine E! Iwe *Da`thūr*?". Iye adati: "Palibe aliyense". Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamukhululukira Iye, tero (adalandira chisilamu ndipo) adayitanira anthu ake ku chisilamu. Ndipo Allah adatewumbenuza mtima wake kuchokera ku kudana ndi Mtumiki (s.a.w) ndikuwasonkhanitsa anthu pa kuchita naye nkhondo, kupita ku kumukonda ndikuwasonkhanitsa anthu kwa Iye.

MAFUNSO

Kodi ndi ziti nkhondo zomwe zidachitika mchaka chachitatu? Nchifukwa chiani Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita ku nkhondo ya Ghatfan? Nchiani chomwe adachita atamva za kutuluka kwake? Kodi nchiani chomwe chidachitika pa nkhondo imenei?

9. NKHONDO YA UHUD

Kutuluka kwa Mtumiki (s.a.w) – Kubwerera kwa anthu anchinyengo – Lamuro la Mtumiki (s.a.w) ndi zotsatira za kutsutsana naye

1. Adatuluka maquraysh kukachita nkhondo ndi Asilamu ndi kukawabwezerera omwe adaphedwa mwa iwo pa nkhondo ya Badr.

2. Ndipo chiwerengero chawo – pamodzi ndi omwe adachita nawo ubwenzi – chinali anthu zikwi zitatu (3000).

3. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita kwa iwo ali ndi anthu chikwi chimodzi (1000), ndipo anabwerera (kumusiya Iye) mnjira Abdullah mwana wa Ubayy limodzi ndi anthu mazana atatu (300) mwa anzake achinyengo.

4. Ndipo pamene adafika Mtumiki (s.a.w) pa phiri la Uhud, adawalamura anthu makumi asanu (50) mwa olasa ndi mipaliro kuti achite linga paphiripo, ndipo adati kwa Iwo: "Musachoke pa phiripa kaya tagonjetsa kapena kugonjetsedwa". Ndipo kenako kumenyana kudayambika pakati pa magulu awiriwo chomwecho Amushrikuna adagonja kuthawa.

5. Ndipo kupambana kudatsala pang'ono kukhala kwa Asilamu, pakadapanda kuti oteteza paphiri (aja) adaswa lamuro la Mtumiki (s.a.w) ndikuchopa pa phiripo, ndipo adatanganidwa ndi ndikutola (katundu osiyidwa ndi adani), pamene adaona kupambana kwa Asilamu.

6. Chomwecho pamene *Khālid* mwana wa *Walīd* adaona kuti phiri lili lopanda munthu, adawathira Asilamu kuchokera kumbuyo kwawo; kunthira kwamphamvu zedi kotero kuti ambiri a iwo adagonja kuthawa.

MAFUNSO

Nchifukwa chiani adatuluka maquraysh pa nkhondo ya Uhud? Chidali chiwerengero chawo chinali chotani? Kodi chinali chotani chiwerengero cha omwe adatuluka ndi Mtumiki (s.a.w)? Kodi adawalamura za chiani Mtumiki (s.a.w) olasa ndi mipaliro? Kodi ndani yemwe adapambana pa nkhondo imenei? Kodi nchiani chomwe chidachitika pambuyo pakuchoka kwawo pa phiri?

10. KULIMBA KWA MTUMIKI (S.A.W) PA NKHONDO YA *UHUD*

Kutha mantha kwake ndi kupirira kwake – Kutemedwa kwa nkhope yake – Kusweka kwa dzino lake – Kuvulala kwa matsaya ake

1. Adalimba nazo Mtumiki (s.a.w) pa nkhondo ya *Uhud* ndipo lidalimba naye limodzi gulu lina la ophunzira ake; ena mwa iwo Abubakr, Umar ndi Ali (*Allah asangalale nawo*).

2. Ndipo ndithu zidamugwera Iye (s.a.w) zipsyinjo zikulu-zikulu, zomwe adazipilira chifukwa cha zomwe Allah adampatsa kuchokera mu kulimba ndi kupirira.

3. Ndithu adalunjika kwa Iye *Ubayy* mwana wa *Khalaf* akufuna kumupha, chomwecho adatenga (s.a.w) nkondo kwa amene adali naye ndipo adamumenya nalo kumenya komwe kudali chifukwa cha kuwonongeka (ndi kumwalira) kwake. Ndipo sadaphepo Iye (s.a.w) munthu wina kupatula Iye moyo wake onse.

4. Ndipo adagwera Iye (s.a.w) mdzenje choncho mawondo ake adavulala ndipo adakomoka. Ndipo adamulasa ndi mwala ena mwa Amushrikuna chomwecho adamutema pa nkhope pake ndipo dzino lake la *Rabā`iyyah* (lachitatu kuchokera pa awiri apakati-kati) ndi awiri a *Thanāyā* (mano awiri a pakati-kati) adasweka.

5. Ndipo adavulalanso ophunzira ake omwe adali kumuteteza (kumutchinga), mabala ambiri zedi.

MAFUNSO

Kodi adalimba motani Mtumiki (s.a.w) pa nkhondo ya *Uhud*? Nchiani chomwe chidamufikira pa nkhondo imenei? Ndani yemwe adalunjika kwa Iye kufuna kumupha? Nchiani chomwe chidamuchitikira pambuyo pa zimenezo? Kodi ophunzira ake adavulala ndi chiani?

11. ANTHU OPHEDWA

1. Ndipo adaphedwa mwa Asilamu pa *Uhud* anthu oposa makumi asanu ndi awiri (70), ndipo adaphedwa mwa Amushrikuna anthu makumi awiri ndi anthu atatu (23).

2. Ndipo Amushrikuna anawaduladula (kuwacheka-cheka) ophedwa a Asilamu kudula-dula koipitsitsa.

3. Ndipo adaphedwa pa nkhondo imenei Hamzah (bamboo ake akulu a Mtumiki s.a.w); adawapusitsa (adawadzidzimutsa) munthu wina dzina lake *Wahshī.*

4. Ndipo adawatumbula pa mimba pawo mzimai wina ndikutenga chiwindi chawo kuti achidye, tero adachinyambita ndipo kenako adachitaya.

5. Ndipo ndithu adadandaula pa Iye Mtumiki (s.a.w), ndipo adalamula za kuwaika (mmanda) onse ofera ku nkhondo muzovala zawo zomwe adaphedweramo.

6. Ndipo pamene Asilamu adabwerera ku Madinah adawachita chipongwe Ayuda ndi anthu achinyengo, ndipo adayankhula kwa abale awo kuti: "***Akadakhala ndi Ife sadafa ndiponso sakadaphedwa***".

MAFUNSO

Tchulani chiwerengero cha ophedwa pa nkhondo ya Uhud? Nchiani chomwe adachita maquraysh pa ophedwa a Asilamu? Ndi ndani odziwika zedi wa omwe adaphedwa pa Uhud? Nchiani chomwe chidachitika kwa Iye pambuyo pa kuphedwa kwake? Nchiani chomwe adachita Mtumiki (s.a.w) ndi ofera pa nkhondo? Nchiani chomwe adanena Ayuda ndi anthu achinyengo pambuyo pa kubwera kwa Asilamu ku Madinah?

12. ZOCHITIKA-CHITIKA

1. Mchaka chachitatu kuchokera mu nsamuko Mtumiki (s.a.w) adamukwatitsa mwana wake *Umm Kulthūm* (r.a) kwa *Uthmān* mwana wa *Affān* (r.a) pambuyo pakuti adamwalira *Ruqayyah* (r.a) ali ndi Iye, (pachifukwa chimenechi amatchedwa kuti mwini kuwala kuwiri (chifukwa cha kukwatira ana awiri a Mtumiki s.a.w).

2. Ndipo mchaka chomwechi Mtumiki (s.a.w) adamkwatira *Hafṣah* mwana wa *`Umar* ibn *Khattāb* ndi *Zainab bint Khuzaymah* (r.a) wa mtundu wachihilāliyyah.

3. Ndipo mchaka chomwechi anabadwa *Hasan* mwana wa *Ali* (r.a).

4. Ndipo momwenso udaletsedwa mowa kuletsedwa kwandithe-ndithe, chifukwa cha kuwononga kwake nzeru, thupi ndi chuma.

5. Udali osaletsedwa kumayambiliro kwa chisilamu ndipo kenako udaletsedwa pang'ono-pang'ono chifukwa cha kuwukonda kwa ma Arabu ndi kuvuta kwa kuwusiya kwake.

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe adakwatitsa Mtumiki (s.a.w) mwana wake Ummu Kuthum? Kodi adamukwatitsa ndi ndani? Kodi Mtumiki (s.a.w) adakwatira ndani mchaka chachitatu? Kodi ndani yemwe anabadwa mchaka chimenechi? Kodi ndi nthawi iti yomwe udaletsedwa mowa? Kodi udali oletsedwa patsogolo pa chisilamu?

CHIDULE CHA CHAKA CHACHITITATU

Idachitika mchaka chachitatu nkhondo ya *Ghatfān* ndi *Bahrān* ndi *Hamrā' al-Asad*, ndipo munalibe monsemo kumenyana kulikonse. Ndipo mchaka chomwecho mudachitika nkhondo ya *Uhud*. Adatuluka maquraysh limodzi ndi abwezi awo pakati pa anthu zikwi zitatu (3000) kuchokera mwa ma Arabu.

Ndipo adafika pa *Uhud* ndicholinga chodzawabwezerera omwe adaphedwa mwa iwo pa Badr. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatuluka kwa iwo pakati pa anthu chikwi chimodzi (1000) – omwe adabwerera mwa iwo *Abdullah ibn Ubayy* ndi athu mazana atatu mwa achinyengo. Ndipo kenako adawalamura Mtumiki (s.a.w) anthu olasa ndi mipiliro kuti asachoke paphiri. Ndipo kumenyana kudayambika chomwecho Amushrikuna adagonja kuthawa. Ndipo kupambana kudatsala pang'ono kukhala kwa Asilamu pakadapanda kuti olasa ndi mipaliro sadaphwanye lamuro la Mtumiki (s.a.w). Chomwecho akavalo a Amushrikuna adawathira nkhondo choncho adagonja ndi kuthawa ambiri a iwo. Ndipo adaphedwa (pa nkhondoyi) anthu oposera makumi asanu ndi awiri (70) mwa iwo, ena mwa iwo ndi Hamzah (r.a); bamboo ake akulu a Mtumiki (s.a.w).

Ndipo *Umayyah ibn Khalaf* adafuna kumupha Mtumiki (s.a.w) chomwecho Mtumiki (s..aw) adamumenya Iye ndi nkondo omwe udakhala chifukwa cha kuwonongeka kwake, ndipo sadaphepo wina kupatula Iye basi. Ndipo adavulala mawondo a Mtumiki (s.a.w), idatemeka nkhope yake ndipo lidasweka dzino ake a *Raba`iyyah* ndi mano awiri a pakati-kati pa mkamwa (*Thanāyā*), ndipo adavulalanso mumtunda mwa matsaya ake. Ndipo adavulalanso omwe adalimba naye limodzi mwa ophunzira ake, mabala ambiri zedi.

Ndipo mchaka chimenechi adakwatitsa Mtumiki (s.a.w) mwana wake *Ummu Kulthūm* (r.a) kwa *`Uthmān ibn Affān*. Ndipo momwemo Iye adamukwatira *Hafṣah* mwana *`Umar ibn Khattāb* ndi *Zaynab bint Khuzaymah* (r.a) wachihilaaliyyah. Ndipo mmenemo anabadwa *Hasan* (r.a), ndipo udaletsedwa mowa kuletsedwa kwandithe-ndithe.

13. CHAKA CHACHINAI KUCHOKERA MU NSAMUKO

Nkhondo ya Banī al-Naḏīr

1. Mchaka chachinai idachitika nkhondo ya *Banī al-Naḏīr* ndi nkhondo ya *Thātu al-Riqā`*[18] ndi nkhondo ya Badr yomaliza, ndipo munalibe (monsemo) kumenyana kulikonse koma nkhondo ya *Banī al-Naḏīr* yokha basi.

2. *Banī al-Naḏīr* ndi mtundu ochokera mwa Ayuda a ku Madinah, omwe pakati pawo ndi pakati pa Asilamu padali mapangano (osiyana-siyana), omwe aliyense mwa iwo amapereka chitetezo kwa wina ndi nzake.

3. (Ulendo wina) anabwera kwa iwo Mtumiki (s.a.w) limodzi ndi ena mwa ophunzira ake, chomwecho lidagwirizana gulu lina la iwo za kumupha, koma Mtumiki (s.a.w) adadziwa za zimenezi choncho adatuluka (kuchoka) kwa iwo, ndipo ophunzira ake adamutsatira.

4. Ndipo kenako adatuma uthenga kwa iwo kuwalamura kuti atuluke mu mzinda (wa Madinah), chomwecho iwo adagonjera koma kenako adakana (kutuluka)[19].

5. Chomwecho adawazungulira (ndi gulu la nkhondo) kufikira adamupempha (kuti awalole) kutuluka, choncho adawalola ndipo adatuluka ndi chuma chawo ndi akazi awo ndi ana awo ndi zomwe adakwanitsa kunyamula pa ngamira zawo, kupatula zida za nkhondo.

---

[18] Adatuluka kupita kumeneko Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa nkhondo ya *Banī Nadīr* ali limodzi ndi omenya nkhondo 700 kukamenyana ndi mafuko a ku Najd, omwe adasonkhana kufuna kuchita naye nkhondo, omwe ndi; *Banū Tha`labah* ndi *Banū Muhārib*, chomwecho pamene adamva za kutuluka kwake adathawa kusiya akazi awo mmbuyo, koma kenako anabwerera ena a iwo kudzamenyana naye, ndipo Asilamu anali kupemphera pemphero la mantha, chomwecho pamene iwo adawaona, Allah adaika mantha mmitima mwawo. Ndipo pankhondo imenei Jibril (a.s) adatsika ndi lamuro la *Salātul-Khawf* (Salah ya nthawi ya mantha), komanso chilolezo cha *Tayammum* (kudziyeretse ndi thodi).

[19] Chomwe chidachititsa kuti akane kutuluka pambuyo pakuti adavomereza nchakuti abwezi awo mwa Amunafiquna (achinyengo a pa Madinah) adawatumizira uthenga kuwawuza kuti; musatuluke mmakomo mwanu, ife tikuthandizani. Choncho Allah adavumbulutsa ndime izi kumudziwitsa Mtumiki (s.a.w) za zimene iwo achita ponena kuti: "Kodi wawaona achinyengo! Akunena kwa abwezi awo amene sadakhulupirire pakati pa anthu a buku kuti; "Ngati mutatulutsidwa (mu nzinda wa Madinah) ndithu ife tidzatuluka nanu limodzi ndipo sitingamvere aliyense za inu mpaka kale-kale. Ndipo ngati mutathiridwa nkhondo ndithu ife tikuthandizani. Koma Allah akuyikira umboni kuti iwo ndionama (pa zimenezi).

Chifukwa cha zimenezi Ayuda adalimba mtima ndipo adakana lamuro la Mtumiki (s.a.w) lakuti atuluke mu Madinah. Koma pamene adapilikitsidwa sadamuone aliyense wodzawathandizira, choncho zidali monga Allah adafotokozera.

MAFUNSO

Ndi nkhondo ziti zomwe zidachitika mchaka cha chachinai? Ndi ndani kodi Banu Nadir? Kodi adachita chiani? Kodi ndi chiani chomwe adawalamura Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kutuluka kwake? Kodi adawachita chiani pambuyo pa zimenezi?

14. ZOCHITIKA-CHITIKA

1. Mchaka chachinai adatsika Jibrīl (a.s) pa nkhondo ya *Thāt al-Riqā`* ndi pemphero la (nthawi ya) mantha, ndipo mnkhondo imeneyinso chidatsika chilolezo cha *Tayammum* (kudziyeretsa ndi dothi).

2. Ndipo mchaka chimenechi adamwalira Zainab (r.a) mkazi wake Mtumiki (s.a.w) ndi *Abū Salamah* (r.a) mwana wa azakhali ake (s.a.w) yemwenso ndi m'bale wake oyamwira naye bele limodzi.

3. Ndipo mchaka chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamkwatira *Ummu Salamah* (r.a).

4. Ndipo mchaka chomwechi anabadwa *Husayn* mwana Ali (r.a).

5. Ndipo mchaka chomwechinso adalamura Mtumiki (s.a.w) *Zaid* mwana wa *Thābit* (r.a) kuti aphunzire kulemba Chiheberi (Chiyuda) ndicholinga chakuti adzimulembera (Iye) kwa iwo Ayuda, ndikuti adzimuwerengera zomwe akulemba kwa Iye.

MAFUNSO

Ndi liti lomwe adatsika Jibrīl (a.s) ndi pemphero la nthawi ya mantha? Nanga ndi liti lomwe chidatsika chilolezo cha *Tayammum*? Ndani yemwe adamwalira mchaka chachinai? Ndindani adamukwatira Mtumiki (s.a.w)? Ndani yemwe anabadwa mchaka chimenechi? Ndi chiani chomwe adalamula Mtumiki (s.a.w) Zaid mwana wa Thabit (r.a)?

CHIDULE CHA CHAKA CHACHINAI KUCHOKERA MU NSAMUKO

Mchaka chachinai idachitika nkhondo ya *Banū Nadīr* (mtundu wa Ayuda omwe udaswa mapangano), chomwecho adawazungulira iwo Mtumiki (s.a.w) ndipo adawatulutsa mMadinah.

Ndipo momwemo idachitika nkhondo ya *Thāt al-Riqā`* ndipo mudalibe kumenyana kulikonse, koma mmenemo mudatsika pemphero la nthawi ya mantha ndi chilolezo cha *Tayammum*. Ndipo momwemo idachitika nkhondo ya Badr yomaliza ndipo munalibe kumenyaana kulikonse. Ndipo momwenso adamwalira *Zainab* (r.a) mkazi wa Mtumiki (s.a.w), ndipo momwemo adamwalira *Abū Salamah*; mwana wa azakhali a Mtumiki (s.a.w) komanso m'bale wake oyamwira naye bele limodzi. Ndipo momwemonso anabadwa Husayn ndipo Mtumiki (s.a.w) adamkwatira *Ummu Salamah* (r.a), ndipo momwemonso adamulamura *Zaid ibn Thābit* (r.a) kuti aphunzire kulemba chiyuda.

(15) CHAKA CHACHISANU PAMBUYO PA NSAMUKO

Nkhondo ya Dūmatul-Jandal – Nkhondo ya Mustaliq – Zifukwa za kulandira Chisilamu kwa mtundu wa Banī Mustaliq

1. Mchaka chachisanu kuchokera mu nsamuko idachitika nkhondo ya *Dūmatul-Jandal*[20] ndipo simudachitike kumenyana kulikonse; chifukwa chakuti adathawa (anthu) omwe anali mmenemo ndipo adasiya (mmbuyo) zifuyo zawo, chomwecho Asilamu adazitenga (monga katundu osiya adani ku nkhondo).

2. Ndipo momwemonso mudachitika nkhondo ya *Banī Mustaliq*[21], (anthu) omwe adasonkhana kuti awathire nkhondo Asilamu.

3. Adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita kwa iwo pakati pa gulu lochuluka zedi chomwecho adawagonjetsa, ndipo Asilamu adawagwira ukapolo akazi awo ndi amuna awo ndi ana awo ndi (kutenga) chuma chawo, ndipo adapha khumi mwa iwo ndipo adawamanga onsewo.

4. Ndipo *Barrah* mwana wa mtsogeleri wawo anali (mmodzi) mwa ogwidwa ukapolo chomwecho adamukwatira Iye Mtumiki (s.a.w) ndipo adamutcha kuti Juwayriyyah.

5. Chomwecho pamene *Banū Mus̱taliq* adamva zimenezi adalandira Chisilamu onse ndipo adasanduka (kukhala) chathandizo kwa Asilamu pambuyo pakuti adali adani awo.

MAFUNSO

Kodi idachitika liti nkhondo ya *Dūmatul-Jandal*? Kodi idachitika liti nkhondo ya *Dūmatul-Jandal*? Kodi Mtumiki adawangonjetsa? Ndani yemwe adamukwatira mwa agwidwa ukapolo awo? Kodi adachita chiani *Dūmatul-Jandal* pambuyo pakuti adamva zimenezi?

[20] Umenewu ndi mzinda omwe uli pakati pa *Shām* ndi Madinah. Mtumiki s.a.w adatuluka kupita kumeneko ali ndi asikali okwana chikwi chimodzi (1000) kukawathira nkhondo anthu akumidzi omwe amachitira zoipa anthu odutsa mnjira yawo, choncho onse adathawa.

[21] Dzina limeneli ndi *laqab* (dzina lodziwika nalo) la munthu wina dzina lake *Juthaymah ibn Sa`d.* nkhondo imenei imatchedwanso kuti *Al-Muraysī*`.

16. NKHANI YA KUSINJIRIRIDWA BODZA

1. Adatuluka limodzi ndi Mtumiki (s.a.w) mwa akazi ake pa nkhondo ya *Banī Mustaliq* Mai olemekezeka Aishah ndi Ummu Salamah (Allah awasangalire).

2. Ndipo mkatikati mwa kubwelera kwa gulu la asikali (ankhondo) adapita mai olemekezeka Aishah (r.a) kukadzithandiza, ndipo pamene adabwerera adataya khoza lake la mkhosi chomwecho adabwerera kukalifuna-funa. Ndipo pamene adalipeza anabwererako ndikuona kuti gulu la asikali latsogola (lapita), choncho tulo lidagonjetsa maso ake (lidamupeza), ndipo adagona pa njira (pomwepo).

3. Ndipo *Safwān* (r.a) adali kuyenda mmbuyo mwa gulu la nkhondolo (kuti) adzifufuza chotaika china chake, chomwecho pamene adafika pamene padali Iye (Aishah) ndikumona, adamudziwa, choncho adagwaditsa ngamira yake ndikumukwezapo popanda kuyankhulana naye liwu lililonse. Ndipo kenako adayenda uku akukoka ngamirayo mpakana adakapezana ndi gulu la asikali (a nkhondowo).

4. Chomwecho (anthu) adamusinjirira Iye (Aishah) kuti wachita zoipa (chiwerewere) ndi *Safwān* (r.a), ndipo amene adatenga gawo lalikulu la kusinjiriraku adali Abdullah ibn Ubayy (yemwe ndi) kapitawo wa anthu achinyengo (Amunafiquna). Ndipo Mtumiki (s.a.w) anali pakati pa kukhulupirira ndi kutsutsa pamene nkhani idafalikira ya Iye[22], mpakana pamene adatsika ma Ayah a kusalakwa kwake (ndi kutalikitsidwa kwake ku zimenezo) mu *Surah Nūr*.

5. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adasangalala ndipo adamupatsa nkhani yabwino ya kuyeretsedwa kwake, ndipo adalamura za kuwakwapula omwe adawonetsera poyera za nkhani ya bodzayo zikoti makumi asanu ndi atatu (80), ndipo iwo (oterowo) adalipo atatu omwe ndi; (*Hamnah* mwana wa *Jah-sh* ndi *Mis̱tah* mwana wa *Uthāthah* ndi *Hassān* mwana wa *Thābit*).

---

[22] Panthawi imeneyi nkuti Iye Aishah (r.a) samadziwa chilichonse chifukwa chakuti pambuyo pa kubwerako ku ulendowu anadwala mwezi watunthu. Choncho Mtumiki (s.a.w) anali kudutsa kwa Iye ndipo amangonena mau akuti "uli bwanji?" basi osawonjezera mau ena aliwonse. Choncho pamene adapezako bwino adawuzidwa za nkhaniyi choncho matenda ake adawonjezekera chifukwa cha maganizo, tero pamene Mtumiki (s.a.w) anabwera kunyumbako Iye adapempha kuti adzikadwalira kwa bambo ake kaye ndipo adamuloleza. Choncho anali kukhalira kumeneko ndipo amangolira usiku onse. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adawafunsa maganizo ophunzira ake kuti achite bwanji pankhaniyi. Choncho Usamah ibn Zaid adati: "Nsungeni mkazi wanu, nsungeni mkazi wanu. Palibe chomwe tikuchidziwa cha iye koma zabwino zokha-zokha basi". Mtumiki adamufunsaso mdzakazi wake (wantchito) ndipo nayenso adaikira umboni oti Iye Aishah sadalakwe chilichonse. Choncho Mtumiki (s.a.w) adabwera kwa Aishah ndipo adamufunsa zoona za nkhaniyi ndikumulangiza kuti alape kwa Allah ngati zili zoona kuti adachitadi choipacho, tero Aishah adalira. Mtumiki (s.a.w) adapitirirabe kumunyengerera Aishah pa zimenezi kufikira mpakana adavumbulutsidwa ma Ayah omuyeretsa ku zoipa ngati zimenezi, omwe ndi mau ake Allah onena kuti: "**Ndithu amene adza ndi bodza (ponamizira Aishah kuti wachita chiwerewere) ndi kagulu kena ka mwa inu. Musayese (nkhaniyi) kuti njoipa kwa inu, koma njabwino kwa inu. Ndipo aliyense wa iwo apeza (chilango) cha tchimo lomwe wachita. Ndipo yemwe watenga gawo lalilikulu la utchimowo mwa iwo adzapeza chilango chachikulu**".

MAFUNSO

Ndani yemwe adatuluka ndi Mtumiki (s.a.w) mwa akazi ake pa nkhondo ya Bani Mustaliq? Nchifukwa chiani Aishah adatsalira mmbuyo mwa gulu la asikali? Ndani yemwe adafikitsa Iye ku gulu la asikali? Kodi adamusinjirira ndi chiani? Kodi Mtumiki adali okhulupirira zomwe zidafalitsidwa za Iye? Kodi nchiani chomwe adachita Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kutsika kwa kuyeretsedwa kwake?

17. NKHONDO YA NKHANDAQ

1. Mchaka chachisanu idachitika nkhondo ya *Nkhandaq* (chingalande), ndipo imatchedwanso kuti *Ahzāb* (makamu kapena magulu).

2. Chifukwa chakuti ambiri mwa mafuko a ma Arabu ndi Ayuda adasonkhana kuti awathire nkhondo Asilamu ndipo adazungulira Madinah.

3. Ndipo chiwerengero chawo chinali anthu zikwi khumi (10,000), omwe amawatsogolera Abu Sufyan mwana wa Harb.

4. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adakumba chingalande mozungulira Madinah kupyolera mu langizo la *Salmān al-Fārsī* (r.a) wachiperezi; chifukwa chakuopa kumenyedwa ndi adani.

5. Ndipo kudapitilira kuzunglilidwa (kwa mzindawo) masiku khumi ndi asanu (15) kufikira pamene liwu lawo la maguluwo lidasokonezeka (lidasemphana pakati pawo).

6. Ndipo Allah adatumiza pa iwo chimphepo champhamvu ndi Asikali omwe sadawawone (angero), chomwe chidazula zichili (za matenti) awo ndikugudubula miphika yawo ndikuthira pa iwo michenga, ndikuwalasa ndi sangalawe (timiyala), chomwecho adawathawa usiku wawo omwewo.

MAFUNSO

Ndi liti lomwe idachitika nkhondo ya Khandaq? Nchifukwa chiani idatchedwa kuti Ahzaab? Tchulani chiwerengero cha magulu omwe adasonkhana? Nchiani chomwe adachita Mtumiki (s.a.w) pofuna kuwatsekereza? Kodi kudapitilira masiku angati kuzungulira? Kodi nchiani chomwe chidachitika kwa iwo pambuyo pa zimenezo?

18. NKHONDO YA BANĪ QURAYDHAH

1. *Banū Quraydhah* ndi mtundu ochokera mwa Ayuda omwe adaswa mapangano pa nkhondo ya Khandaq ndipo adaonetsa udani kwa Asilamu.

2. Chomwecho pamene adabwerera Mtumiki (s.a.w) kuchokera ku nkhondo ya Khandaq, Allah adamulamura za kuwathira nkhondo ndi kuliyeretsa dziko lake kwa iwo.

3. Chomwecho adatuluka kupita kwa iwo Mtumiki (s.a.w) ali ndi anthu zikwi zitatu (3,000), choncho adawazungulira masiku makumi awiri ndi mphambu zisanu (25).

4. Chomwecho adagonjera (ndi kudzipereka) pambuyo pake, ndipo Sa`id ibn Mu`ādh adagamula za kuwapha amuna awo ndi kuwatenga ukapolo akazi ndi an awo.

MAFUNSO

Kodi Banu Quraydhah ndi ndani? Nchiani chomwe Allah adamulamura nacho Mtumiki (s.a.w)? Ndani omwe adatuluka naye limodzi? Nchiani chomwe adachita pambuyo pa kuwazungulira kwawo? Nchiani chomwe adalamura Mtumiki (s.a.w)?

19. NKHANI YA ZAID (R.A) NDI ZAINAB (R.A)

1. Adafunsira banja Mtumiki (s.a.w) Zainab *bint Jahsh* (r.a) (kumufunsilira) *Zaid ibn Hārithah* (r.a) chomwecho Iye adakana ndipo nawonso akubanja lake adakana.

2. Chomwecho Allah adavumbulutsa mau awa: "**Ndipo sikoyenera kwa wokhulupirira wachimuna ndi wokhulupirira wachikazi (kuti pamene) Allah ndi Mtumiki wake walamula chinthu, iwo nkukhala ndi chifuniro pa zinthu zawo. Ndipo amene akunyoza Allah ndi Mtumiki wake ndithu wasokera kusokera kowonekera**".

3. Pamenepo adalola chomwecho Zaid (r.a) adalowa kwa Iye, koma kuti Iye (Zainab) adayamba kudzikweza kwa Iye chifukwa cha ulemelero wake ndi mtundu wake, chomwecho Iye (Zaid) adakadandaula za Iye kwa Mtumiki (s.a.w).

4. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamulamura Iye za kupirira naye, chomwecho adapilira mpakana moyo wake udathinidwa choncho adamufotokozera Mtumiki (s.a.w) za chitsimikizo chake cha kumusiya banja.

5. Chomwecho Allah adamulamura Mtumiki (s.a.w) za kumukwatira Iye pambuyo pa kumusiya kwake (banja); pofuna kusunga ulemelero wake, komanso kufuna kuchotsa mkangano ndi kusagwirizana, ndikufuna kuthetsa chikhalidwe cha *Tabannī* (kumulera mwana ndikumuchita kukhala ngati mwana wako weni-weni womubala).

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adamufunsilira banja Zainab kwa ndani? Kodi ndi chiani chomwe chidavumbulutsidwa pa zimenezo? Kodi abale ake adalola pambuyo pa kuvumbulutsidwa kwake? Nchiani chomwe Mtumiki (s.a.w) adamulamura Iye pambuyo pakuti adakadandaula za Iye? Nchiani chomwe Allah adamulara Mtumiki wake pambuyo pakuti Zaid adatsimikiza za kumusiya banja?

20. KUTHETSA CHIKHALIDWE CHA TABANNĪ

1. Mtumiki (s.a.w) adali atamuchita Zaid ibn Hārithah kukhala ngati mwana wake (odzibalira) kotero kuti adamulumikiza ndi mtundu wake, monga momwe chidalili chikhalidwe cha ma Arabu pakuchita *Tabannī*.

2. Chomwecho pamene Allah adamulamura Iye za kumukwatira Zainab, Iye adati kwa Zaid: "**Gwirizana ndi mkazi wako (musungebe) ndipo umuope Allah**". Ndipo Iye (Mtumiki s.a.w) anabisa lamuro la Allah uku akudziwa kuti zikuyenera kuchitakabe basi.

3. Chifukwa chakuti Iye adaopa kuti ma Arabu angayankhule kuti: "**Muhammad wakwatira mkazi osiyidwa banja ndi mwana wake (yemwe)**".

4. Chomwecho Allah adavumbulutsa pa zimenezo (mau awa): "**Choncho pamene Zaid adamaliza chilako-lako chake pa mkazi ameneyo, tidakukwatitsa Iwe kuti pasakhale masawutso pa Asilamu pokwatira akazi a ana awo ongowalera chabe ngati anawo atamaliza zilakolako zawo pa akaziwo, ndipo lamuro la Allah ndi lochitika basi (palibe chingalepheretse kuti lisachitike)**". Ndipo kenako (Allah) adaletsa *Tabannī* kwa Asilamu chifukwa cha zosawutsa zomwe zili mmenemo, ndipo adavumbulutsa (mau awa): "**Muhammad sali tate wa aliyense wa amuna anu koma Iye ndi Mtumiki wa Allah ndiponso otsiriza wa Aneneri, ndipo Allah Ngodziwa chilichonse**". Ndipo kuchokera panthawi imeneyi lidasanduka dzina la Zaid (kuti) "Zaid mwana ibn Harithah" mmalo mwa "Zaid mwana wa Muhammad".

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adali atamutenga ngati chiani Zaid mwana wa Harithah? Nchiani chomwe adanena kwa Zaid pamene Allah adamulamura Iye za kumukwatira Zainab? Nchifukwa chiani sadamukwatire? Nchiani chomwe chidavumbulutsidwa pambuyo pa zimenezo?

21. AYAH YA HIJAB NDI KUKAMIZIDWA KWA HAJJ

1. Mchaka chachisanu idatsika Ayah ya Hijab (lamuro la kudziphimba), yomwe ndi yapadera-dera kwa akazi a Mtumiki (s.a.w), omwe ndi mau ake (Allah onena kuti): "**Ndipo Inu mukamawafunsa akazi ake za ziwiya, afunseni uku muli kuseli kwa chotsekereza. Kuchita zotere kuyeretsa mitima yanu ndi mitima yawo**". Koma akakhala (akazi ena) osakhala akazi ake, ndiye adalamulidwa za kuzyolitsa/kugwetsa maso, ndikuti asaonetsere poyera zodzikongoletsera zawo.

2. Ndipo Hijab imagawidwa mitundu itatu: mtundu umodzi ndi wapadera-dera kwa akazi a Mutmiki (s.a.w), ndipo mitundu iwiri imaphatikiza akazi a Mtumiki (s.a.w) ndi ena (osakhala iwo).

3. Chomwecho mtundu oyamba ndiwakuti adziphimbe mkazi thupi lake lonse mpaka nkhope yake ndi (zikhatho za) manja ake, ndipo imenei ndi yomwe Ayah ya Hijab idatsika kudzakamba zokhudza iyo, pankhani yokhudzana ndi akazi a Mtumiki (s.a.w), ndipo imenei ndi yapadera kwa iwo.

4. Yachiwiri ndiyakuti mkazi adziphimbe thupi lake lonse kupatula nkhope ndi (zikhatho za) manja awiri. Ndipo ma Ulama ena adawonjezera (kuphimba) mapazi awiri kwa (azimai) osawuka amene (amatanganidwa) kugwira ntchito mminda, ndipo zimenezi ndi mau ake (Allah onena kuti): "**E! Iwe Mneneri! Uza akazi ako ndi ana ako akazi ndi akazi a Asilamu kuti adziphimbe ndi nsalu zawo (akamatuluka mnyumba zawo).** (*Surah Ahzāb*). Ndi kuyankhulanso kwake (Allah konena kuti): "**Ndipo asawonetse (poyera) zomwe amazikongoletsa nazo kupatula zomwe zaonekera poyera (popanda cholinga chotero). Ndipo afunde kumutu mipango yawo mpaka mzifuwa zawo**". (*Surah Nūr*). Ndipo (Hijab) imenei ndi ya onse.

5. Yachitatu ndiyakuti; pasakhale kusakanikirana pakati pa akazi ndi amuna – kupatula (ngati) ali limodzi ndi Mahram (m'bale wake yemwe sangakwatirane naye monga mlongo wake kapena bambo ake). Ndipo imeneyinso ndi yokhudza onse; akazi a Mtumiki (s.a.w) ndi ena osakhala iwo, chifukwa cha kuyankhula kwake Mtumiki (s.a.w) (konena kuti): "**Asakhale awiri-wiri mamuna ndi mkazi kupatula ngati (mkaziyo) ali limodzi ndi m'bale wake obadwana naye**)". [Bukhari]. Ndipo imeneyinso ndi yokhudza onse.

6. Ndipo mchaka chimenechi adakakamizidwa mapemphero a Hajj kwa omwe angakwanitse njira yokafikira kumeneko, kuti Asilamu adzisonkhana ku Makkah ndikuti adziwane ndi kuchita umodzi.

MAFUNSO

Kodi Ayah ya Hijab idatsika liti? Kodi Hijab imagawidwa mitundu ingati? Kodi mtundu oyamba ndi uti? Nanga wachiwiri? Nanga wachitatu? Kodi Hajj idakakamizidwa liti?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHACHISANU PAMBUYO PA NSAMUKO

Mchaka chachisanu kuchokera mu nsamuko idachitika nkhondo ya *Dūmatul-Jandal*, ndipo simudachitike kumenyana kulikonse. Kenako nkhondo ya *Banī Musṯaliq* chomwecho anaphedwa (mmenemo) anthu khumi ndipo anagwidwa ukapolo anthu ena onse otsara. Ndipo *Juwayriyyah bint Hārith* mwana wa mtsogeleri wawo adali mmodzi mwa ogwidwa ukapolo chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamukwatira, ndipo kumukwatira kwake kudakhala chifukwa chopangitsa kulowa chisilamu kwa anthu ake.

Ndipo munkhondo yomweyi adasinjiriridwa Mai olemekezeka Aishah (r.a) (za kuchita zoipa ndi) *Safwān* mwana wa *Mu`attal* (r.a), chomwecho Qur'an idamuyeretsa (ku zimenezo).

Ndipo mchaka chomwechi idachitika nkhondo ya *Nkhandaq*; adasonkhana maquraysh limodzi ndi ena ochokera mwa ma Arabu ndi Ayuda kuti awathire nkhondo Asilamu, ndipo chiwerengero chawo chinali anthu zikwi khumi (10,000). Chomwecho Asilamu adakumba chingalande mozungulira Madinah, ndipo kuzungulilidwa (ndi adaniko) kudapitilira masiku khumi ndi asanu (15), ndipo chomwecho Allah adatumiza pa iwo chimphepo ndi asikali omwe iwo sadawaone ndipo adabwerera popanda kupeza chomwe amafuna (manja-manja).

Ndipo momwemonso idachitika nkhondo ya *Banī Quraydhah* chifukwa cha chinyengo chawo pa (kuswa) pangano, chomwecho adawapha ndikuwagwira ukapolo akazi awo ndi ana awo.

Ndipo momwemo adakwatira Mtumiki (s.a.w) *Zainab bint Jahsh* (r.a) pambuyo pakuti adamusiya banja *Zaid ibn Harithah* (r.a), ndipo chidathetsedwa chikhalidwe cha *Tabannī*. Ndipo momwemo idakakamizidwa Hajj.

(22) CHAKA CHACHISANU NCHIMODZI PAMBUYO PA NSAMUKO

Nkhondo zake - Kulowa Chisilamu kwa Thumāmah ndi kuvomereza kwake

1. Mchaka chachisanu ndi chimodzi (6) idachitika nkhondo ya *Banī Lahyān*[23] chifukwa cha kuchita kwawo chinyengo[24], ndipo panalibe kumenyana kulikonse chifukwa chakuti iwo adathawa.

2. Ndipo momwemo idachitikanso nkhondo ya *Al-Ghābah*[25] (nkhalango); mudachitaka mkati mwake kulasana ndi mipaliro chapatali (popanda kuyandikirana bwino-bwino), (ndipo) adaphedwa mkati mwa zimenezi Msilamu mmodzi ndi Amushrikina awiri.

3. Ndipo momwemo idachitika nkhondo ya *Hudaybiyyah*[26] ndipo simudachitike kumenyana kulikonse, chifukwa chofuna kuteteza kupatulika ndi ulemelero wa nyumba yopatulika (Ka`bah).

4. Ndipo mchaka chomwechi adalowa Chisilamu *Thumāmah*[27] mwana wa *Uthāl* pambuyo pakuti Mtumiki (s.a.w) adachita naye (ndikumuonetsa) mapeto a makhalidwe apamwamba.

5. Ndipo pambuyo pa kulandira kwake Chisilamu adati kwa Mtumiki (s.a.w): "**Ndikulumbira Allah E! Iwe Muhammad! (Ndithu) panalibe pamwamba pa nthaka nkhope yodedwa zedi kwa ine kuposa nkhope yako. Ndikulumbira Allah padalibe padziko lonse chipembedzo chodedwa kwambiri kwa ine kuposa chipembedzo chako, koma ndithu (tsopano) chasanduka kukhala chipembedzo chokondeka zedi kwa ine (kuposa zipembedzo zonse). Ndikulumbira Allah, padalibe dziko lodedwa zedi kwa ine kuposa dziko lako, koma ndithu (lero) dziko lako lasanduka dziko lokondeka zedi kwa ine kuposa maiko onse".**

---

[23] Dzina la mtundu wina wa chiarabu.

[24] Zidali chomwecho chifukwa chakuti Mtumiki (s.a.w) adawatumizira munthu wina (ophunzira wa Mtumiki s.a.w) dzina lake Āsim mwana wa Thābit (r.a) kuti akawaphunzitse chipembedzo chomwecho Iwo adamupha. Ndipo Iye adali limodzi ndi gulu (la anzake) omwe 8 mwa Iwo adawapha ndipo awiri ena adawagulitsa (ngati akapolo) kwa anthu a ku Makkah ndipo (anthu aku Makkawo) adawaphanso. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita kwa Iwo ndi anthu (asikali) 200 apa zokwera, chomwecho sadawepeze (anthuwo).

[25] Amenewa ndi malo omwe ali pakati pa Makkah ndi Madinah. Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita kumeneko ali ndi anthu (asikali) mazana asanu (500) kukamenyana ndi Aluya omwe adapha ndi kulanda ngamira za Mtumiki (s.a.w) ndipo adapha mwana wa Abī Thar (r.a). Ndipo (mmenemo nkuti) Mtumiki (s.a.w) anali atamuchitira zabwino mtsogeleri wawo (yemwe ndi `Uyaynah mwana wa Hisn) choncho adamupatsa nthaka (malo), koma Iye sadayamike ubwino umenewu ndipo adachita zomwe adachitazo.

[26] Hudaybiyah ndi chitsime chomwe chili pakati pa Makkah ndi Madīnah.

[27] Lidamugwira gulu laling'ono la asikali ankhondo mnjira ndipo lidabwera naye kwa Mtumiki (s.a.w) chomwecho adamuzindikira ndipo adalowa Chisilamu, ndipo pambuyo pa kulowa kwake Chisilamu adabwerera kwawo ku Yamamah. Ndipo adadutsira ku Makkah kukachita Umrah ndikuwonetsera kumeneko Chisilamu chake. Ndipo pamene adabwerera kwawo adaletsa kuti mbewu za ku Yemeni zisamafike kwa Amushrikin kufikira alowe Chisilamu. Chomwecho maquraysh adamupempha chithangato Mtumiki (s.a.w) ndipo Iye adawachitira chifundo. Ndipo adatumiza uthenga kwa Thumamah (r.a) kuti abwezeretse kwa Iwo zomwe zimawafikira, chomwecho Iye adachita zimenezo.

MAFUNSO

Kodi nkhondo ya Bani Lahyan idachitika mchaka chanji? Kodi nkhondo ya al-Ghabah idachitika chaka chanji? Kodi nkhondo ya Hudaybiyyah idachitika chaka chanji? Ndani yemwe adalandira chisilamu mchaka chimenechi? Adati chiani kwa Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kulandira chisilamu?

23. NKHONDO YA *HUDAYBIYAH* NDI MALONJEZANO A CHIYANJO CHA ALLAH (*RIDWĀN)*

1. Chifukwa (chomwe chidayambitsa nkhondo imenei)[28] nchakuti Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita ku Makkah kukachita mapemphero a Umrah osati nkhondo ayi ali limodzi ndi anthu chikwi chimodzi ndi mazana asanu (1,500) kuchokera mwa ma *Muhajirūn* ndi ma *Ansār* popanda zida (za nkhondo). Choncho pamene maquraysh adadziwa za kutuluka kwake adasonkhana kuti amutsekereze kufika ku nyumba ya Allah yolemekezeka.

2. Koma kuti simudachitike mkati mwake kumenyana kulikonse: chifukwa cha kulemekeza kupatulika kwa nyumba yopatulika yomwe Allah adaichita kukhala yopatulika ndi yotetezeka.

3. Ndipo pamene Mtumiki (s.a.w) adafika pa Hudaybiyyah, maquraysh adatumiza kwa Iye nthumwi kukamufunsa cholinga cha kubwera kwake.

4. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatumiza Uthman (r.a) kwa iwo kuti akawadziwitse cholinga chake, ndipo adawapatsa nkhani yabwino (Asilamu ofowoketsedwa omwe adatsekerezedwa ndikukanizidwa kusamuka ku Makkah) za kuyandikira kwa chipulumutso (chigonjetso), ndikuti ndithu Allah achipititsa patsogolo chipembedzo chake.

5. Chomwecho pamene Iye atafika maquraysh adamutsekera choncho zidafalikira pakati pa Asilamu kuti Uthman waphedwa.

6. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawaitana anthu kuti adzachite malonjezano, chomwecho adamulonjeza pansi pa mtengo wina kumeneko kuti; Iwo sangathawe (ngati zitavuta nthawi yankhondo). Ndipo malonjezano amenewa amatchedwa "**Malonjezano a Ridwān (chiyanjo cha Allah)**".

[28] Mtumiki (s.a.w) adalota kutulo kwake atalowa mu mzinda wa Makkah Iye limodzi ndi ophunzira ake; (ena a Iwo) atameta tsitsi ena atayemula. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawauza Asilamu kuti Iye akufuna kukachita Umrah, ndipo adatuluka limodzi ndi omwe adali naye mpaka adafika kumusi zedi kwa Hudaybiyah. Chomwecho pamene maquraysh adamva za kufika kubwera kwake adamutumizira nthumwi kuti zikamufuse chomwe chamudzetsa. Ndipo pakati pa nthumwi zamwo panali Urwah mwana wa Mas`ud wa Mtundu wa Thaqif; adadza kwa Mtumiki (s.a.w) ndipo adati: "E! Iwe Muhammad! Wasonkhanitsa anthu onyozeka ndi opanda pake ndipo wabwera nawo kwa anthu ako ndi abale ako kuti usawasokoneze pakati pawo. Ndithudi maquraysh alumbiral (ndikutsimikiza) kuti usalowe mzinda wa Makkah chaka chino". Ndipo kenako Urwah adabwerera pambuyo pakuti adaona zomwe amachita ma Sahabah (r.a) kwa Mtumiki (s.a.w), pakuti sanali kuchita Wudu koma kuti ma Sahabah (r.a) adali kulimbirana ndikumadzipaka madzi omwe akuchoka pa thupi lake. Ndipo akakhala pansi onse amatsitsa mau awo (kukhala chete) pamaso pake, ndipo sanali kunyamula maso awo kumupenyetsetsa. Ndipo pamene (Urwah) adafika kwa maquraysh adati kwa Iwo: "Ndidamudzerapo Kisra (mfumu ya ku Persia) mu ufumu wake, ndipo ndidamudzeraponso Qasysar (mfumu ya ku Romu) mu ufumu wake; koma sindidaonepo mfumu pakati pa anthu ake (ingafanane) ndi Muhammad pakati pa ophunzira ake, omwe sangamupereke chifukwa cha chinthu chilichonse. Chomwecho onani momwe mungachitire pakuti ndithu Iye wapereka pamaso panu zolungama chomwecho ziloleni. Ndipo ndithu Ine ndikukufunirani zabwino (pa kukulangizani) ndipo ndikuopa kuti simungamugonjetse".

MAFUNSO

Kodi chomwe chidachititsa nkhondo ya Hudaybiyyah nchiani? Kodi padachitika kimenyana kulikonse pakati pa magulu awiriwa? Kodi maquraysh adatumiza chiani kwa Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kufika kwake pa Hudaybiyyah? Ndani yemwe Mtumiki (s.a.w) adamutumiza kwa Iwo? Kodi maquraysh adamuchita chiani Uthman? Nchiani chomwe adachita Mtumiki (s.a.w) pamene idafala mbiri ya kuphedwa kwa Uthman?

24. MGWIRIZANO WA CHIYANJANO WA HUDAYBIYAH

1. Pamene maquraysh adadziwa za malonjezano a *Ridwān* adadziopera[29] chomwecho adamumasula (ndikumutumiza) Uthman (r.a) ndi omwe adali naye limodzi.

2. Ndipo adapempha chiyanjano (mgwirizano) choncho (chiyanjanocho) chidachitika mogwirizana ndi fundo zomwe maquraysh adafuna kudzera pa lilime la nthumwi yawo.

3. Zomwe ndi: Kusiya kumenyana (nkhondo) kwa zaka khumi (10), ndikuti anthu atetezeke kwa wina ndi nzake (pasakhale udani uliwonse), ndikuti Iye (Mtumiki s.a.w) abwerere chaka chino (asakafike ku Ka`bah), ndikuti asamawabweze omwe awadzera (iwo maquraysh) kuchokera mwa Asilamu, ndikuti Mtumiki (s.a.w) adziwabweza omwe amudzera (kuthawa) kuchokera kwa maquraysh[30].

4. Chomwecho Asilamu adathinidwa ndi fundo zimenezi, maka-maka kuwaletsa kuti asachite *Tawāf* pa nyumba ya Allah (Kabah).

5. Ndipo mkati-kati mwa kubwelera kwake Mtumiki (s.a.w) idavumbulutsidwa kwa Iye Surah al-Fat-h, chomwecho adasangalala Asilamu chifukwa cha nkhani yabwino ya kugonjetsedwa kwa Makkah, ndipo adadziwa kuti palibe kuchitira mwina iwo adzailowa ali otetezeka uku atameta (tsitsi) mmitu mwawo.

---

[29] Pa nkhondo imenei adatsika mau ake (Allah) Wapamwamba-mwamba (onena kuti): "**Ndithu amene akukulonjeza ndiye kuti akulonjeza Allah, dzanja la Allah lili pamwamba pa manja awo**". Komanso (adatsikanso) mau ake Allah (onena kuti): "**Ndithu Allah adawanja okhulupirira pamene adagwiriana nawe chanza pansi pa mtengo pomwe amakulonjeza…**". Ndipo Umar (r.a) adalamura za kuwudula mtengo wa Ridwān (chiyanjo) nthawi ya utsogoleri wake pamene adaona kuti anthu akumatenga madalitso ku mtengowo (powukhudza ndi zina).

[30] (Masahabah) adati kwa Mtumiki (s.a.w): "Zitheka bwanji kuti tidziwabwezera Iwo (maquraysh) omwe abwera kuchokera kwa Iwo pomwe Iwo asamabweze kwa Ife omwe awadzera kutuluka Chisilamu?". Chomwecho Iye (s.a.w) adati: "Yemwe wapita (kwa Iwo) kuchokera kwa Ife (ndiye kuti) Allah wamutalikitsa ndi Ife, koma yemwe watidzera kuchokera mwa Iwo ife ndikumubwezera kwa Iwo ndiyekuti Allah amupangira danga ndi njira yotulukira mmavuto amenewo".

6. Pambuyo pa zimenezi Asilamu adasanduka afulu; adali kupita ndikubwelera momwe angafunire, ndipo kufikira kwake kwa Mtumiki (s.a.w) (mmadera osiyana-siyana) kudakula zedi.

7. Ndipo adalemba (makalata) kupita ku maiko oyandikana ndi dziko la ma Arabu; kuwaitanira ku Chisilamu, choncho ena a iwo adalandira Chisilamu monga *Najāshi* (r.a) mfumu ya ku *Habashah*. Ndipo alipo ena omwe adayankha yankho labwino monga *Hiraql* Kaisara (mtsogoleri) wa ku Roma ndi *Muqawqis* mtsogeleri wa Iguputo. Ndipo alipo ena omwe adayankha yankho loipa ndikuinyoza nthumwi ya Mneneri (s.a.w) monga *Al-Hārith* mwana wa *Shammar* wa mtundu wa *Ghassān* ndi *Kisrā* (mtsogolera) wa Aperezi (Persia).

MAFUNSO

Kodi maquraysh adachita chiani atadziwa za malonjezano a Ridwān? Kodi fundo za mgwirizano ndi ziti? Kodi nchiani chomwe chidatsika kwa Mtumiki (s.aw) mkati mwa kubwerera kwake kuchokera ku Hudaybiyyah? Kodi Asilamu adasanduka motani pambuyo pa chiyanjano chimenecho? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiyani pambuyo pa zimenezi?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHACHISANU NCHIMODZI PAMBUYO PA NSAMUKO

Mchaka cha chisanu nchimodzi (6) idachitika nkhondo ya *Banī Lahyān* chifukwa cha kuchita kwawo chinyengo ndipo munalibe kumenyana kulikonse. Ndipo kenako (idachitika) nkhondo ya *Al-Ghābah* (yomwe) mudachitikamo kulasana ndi mipiliro chapatali (popanda kukumana kapena kuyandikirana kweni-kweni). Ndipo kenako (idachitika) nkhondo ya *Hudaybiyah*. Adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita kumeneko ali limodzi ndi anthu 1,500 mwa ophunzira ake opanda zida (za nkhondo), chomwecho maquraysh adamuletsa (kukafika ku nyumba ya Ka`bah). Choncho Iye adatumiza *Uthmān* (r.a) kuti akawadziwitse za cholinga chake (s.a.w), chomwecho maquraysh adamutsekera ndipo zidafalikira pakati pa Asilamu kuti Iye waphedwa.

Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatenga malonjezano kwa ophunzira ake pansi pa mtengo wa Ridwān (chiyanjo cha Allah) pa fundo yakuti: Iwo sangathawe (ngakhale zitavuta) pa nkhondo (yobwezera kuphedwa kwa *Uthmān*), choncho iwo (maquraysh) adaopa. Ndipo udachitika pakati pa magulu awiriwa (Asilamu ndi maquraysh) mgwirizano wakuyanjana pa fundo (zomwe) zina mwa izo (ndi zakuti); kuimikira nkhondo kwa zaka khumi ndi kuwapatsa chitetezo anthu, chomwecho Asilamu adabwerera.

Ndipo idavumbulutsidwa mkati mwa kubwelera kwa Mtumiki (s..aw) Surah Al-Fat-h, ndipo tero adasangalala Asilamu. Ndipo pambuyo pa mgwirizano wa chiyanjanowu Asilamu adakhala afulu; amapita ndi kubwelera momwe angafunire.

Ndipo kudatambasuka kufikira kwa Mtumiki (s.a.w) (ku madera osiyana-siyana) choncho adalemberana nawo makalata mafumu: kuwaitanira ku chipembedzo chachisilamu ndipo adalandira Chisilamu ena mwa iwo.

25. CHAKA CHACHISANU NDI ZWIRI (7) PAMBUYO PA NSAMUKO

1. Mchaka chachisanu ndi ziwiri (7) idachitika nkhondo ya Khaybar ndi nkhondo ya *Wādi al-Qurā*.

2. Adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita ku Khaybar kukamenyana nkhondo ndi okhala kumeneko (omwe ndi) *Banū Nadīr*, omwe adali okhwirizira zedi magulu (anzawo) pa tsiku la (nkhondo ya) *Khandaq*.

3. Chomwecho pamene Asilamu adafika ku malinga a Khaybar, adanyamula mau awo (kufuwula) ndi Takbīr (kulikweza dzina la Allah) ndi Duwa (kumupempha), chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati kwa iwo: "**Dekhani ndipo tsitsani mau anu, pakuti inu simukuitana (ndikumupempha) yemwe ali gonthi (osamva) kapana yemwe ali kutali nau. Ndithu inu mukuitana ndi kumupempha yemwe ali Wakumva zedi, Oyandikira zedi (yemwe ndi Allah)**". [Bukhari/Muslim].

4. Ndipo kenako Asilamu anadula (ndi kugwetsa) mitengo ya kanjedza (tende) ya Ayuda, ndipo adawazungulira masiku asanu ndi limodzi (6) kuti awakakamize kudzipereka.

5. Ndipo tsiku lachisanu ndi chiwiri (7) Mtumiki (s.a.w) adapereka mbendera (ya gulu la asikali) kwa *Alī* mwana wa *Abī Tālib*, ndipo iye anali kudwala maso ake, choncho Mtumiki (s.a.w) adalavulilamo (mmasomo), tero Allah adawachiza maso akewo kukhala ngati kuti sadali ndi vuto lililonse.

6. Ndipo kenako Asilamu adaithira nkhondo pa Khaybar mpakana adaigonjetsa ndipo adawapirikitsa okhalamo ake, ndipo adapeza mmenemo katundu wambiri wa kunkhondo ndipo zina mwa izo ndi; ziwiya za mtofu (Aluminiyamu) ndi zadothi zapamwamba zedi. Mtumiki (s.a.w) adati kwa iwo (Asilamu): "**Zitsukeni ndipo mungathe kuphikiramo**".

MAFUNSO

Ndi nkhondo ziti zomwe zidachitika mchaka cha 7 kuchokera mu nsamuko? Nchifukwa adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita ku Khaybar? Asilamu adachita chiani atafika ku Khaybar? Nchiani chomwe adachita pambuyo pa zimenezo? Ndani yemwe Mtumiki (s.a.w) adamupatsa mbendera ya nkhondo? Nchiani chomwe chidachitika pambuyo pake?

26. KUGONJETSEDWA KWA *FADAK*, NDI MGWIRIZANO WA CHIYANJANO WA *TAYMĀ'*, NDI NKHONDO YA *WĀDI AL-QURĀ*.

1. Pambuyo pa kugonjetsa Khaybar, Mtumiki (s.a.w) adalamura Ayuda a (dera la) *Fadak* za kugonjera chomwecho adachita naye mgwirizano wa chiyanjano pa kuteteza mwazi wawo ndikuti chuma chawo chisiidwe (osalandidwa).

2. Ndipo pamene Ayuda a (dera la) *Taymā'* adamva zomwe zidawagwera Ayuda a Khaybar (nawonso) adachita naye Mtumiki (s.a.w) mgwirizano wa chiyanjano kuti adzipereka *Jizyah* (nsonkho), ndipo adakhala mmaiko mwawo mwamtendere.

3. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adawaitaniranso Ayuda a *Wādī al-Qurā* ku kugonjera, chomwecho iwo adakana ndipo adawathira nkhondo Asilamu.

4. Chomwecho Asilamu athirana nawo nkhondo ndipo adapeza katundu wa kunkhondo ochuluka zedi, ndipo kenako Mtumiki (s.a.w) adaisiya nthakayo (kuwasiira) eni ake, kuti (angathe) kumalimamo mbewu ndikumapereka theka la zokolola zake (kwa Mtumiki s.a.w). Chimodzimodzinso ndi momwe adachitira ndi nthaka ya Khaybar.

5. Chomwecho Asilamu adatetezeka ku zoipa za Ayuda ndipo adabwerera ku Madinah ali othandizidwa (ndi Allah) komanso opambana.

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani pambuyo pa kugonjetsa Khaybar? Nchiani chomwe adachita Ayuda a Tayma pambuyo pakumva zomwe zidawagwera Ayuda a Khaybar? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani pambuyo pake? Kodi Asilamu adamenyana nawo nkhondo? Kodi Asilamu adakhala bwanji pambuyo pake?

27. UMRAH YOBWEZA

1. Pamene udaoneka mwezi wa *Thul-Qa`dah* mchaka chachisanu nchiwiri (7), adatuluka Mtumiki (s.a.w) limodzi ndi omwe adali naye kuti akabweze Umrah yawo yomwe Amushrikuna adawaletsa kuchita pa mgwirizano wa chiyanjano wa Hudaybiyah.

2. Ndipo ulendo umeneu adatenga limodzi ndi Iye zida (za nkhondo) powopa chinyenga cha maquraysh.

3. Ndipo pamene Iye adafika pa *Marr al-Dhahrān* maquraysh adadziwa za kubwera kwake chomwecho adachita mantha ndipo adamutumizira anyamata ochokera mwa iwo.

4. Ndipo iwo (anyamatawo) adati kwa Iye: “E! Iwe Muhammad! Sudadziwikepo ndi chinyengo (cha kuswa pangano) uli wamng’ono ngakhalenso uli wamkulu, ndipo ndithu ife sitidachite chilichonse (chakuswa pangano)”. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawawuza kuti Iye akufuna (kuchita) Umrah osati kumenyana nawo.

5. Ndipo pamene kudayandikira kulowa kwa Asilamu mu Makkah, Amushrikuna adatulukamo posafuna kuwawona akuchita *Tawāf* (kuzungulira Ka`bah) pa nyumba yopatulika.

6. Chomwecho Asilamu adalowa ndi zida zawo mwamtendere (ali otetezeka) atameta (tsitsi) mmitu mwawo komanso atayepula, ndipo kenako adabwerera pambuyo pa masiku atatu.

MAFUNSO

Kodi ndi liti lomwe adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita kuchita Umrah yobweza? Nchiani chomwe adatenga naye limodzi ulendo umenewu? Nchiani chomwe adachita maquraysh pamene adadziwa za kubwera kwake? Nchiani chomwe anyamata aja adanena kwa Iye? Nchiani chomwe chomwe Amushrikuna adachita pamene Asilamu adayandikira ku Makkah? Kodi Asilamu adalowa bwanji mu Makkah?

28. ZOCHITIKA-CHITIKA

1. Adapereka mphatso pa tsiku la kugonjetsedwa kwa Khaybar mzimai wina wachiyuda ya mwendo wa nkhosa wothiridwa poisoni kwa Mtumiki (s.a.w), chomwecho Iye adatenga pisi ya mnofu mmenemo koma kenako adailavula pambuyo pakuti adadziwitsidwa kuti ndi yothiridwa poizoni, ndipo ophunzira wina anadya kuchokera mmenemo ndipo adamwalira nthawi yomweyo. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adachita *Hijāmah* (kuchotsa magazi mthupi) ndipo adamuitanitsa mzimai yemwe adachita chinthu chimenechi kuti amufunse chomwe chidamuchititsa zimenezi, chomwecho Iye adayankha kuti: "Ndidaganiza kuti ngati Iye ali Mneneri ndiyekuti sizimpatsa vuto lililonse, ndipo ngati ali wabodza ndiyekuti Allah atipumitsa kwa Iye (pakumupha ndi poizoniyo)". Chomwecho Iye adamukhululukira.

2. Pambuyo pa kugonjetsa Khaybar adakwatira Mtumiki (s.a.w) *Safiyyah* mwana wa Huyiyy ndipo Iye adalandira Chisilamu.

3. Ndipo Iye (s.a.w) ali ku Khaybar adaletsa ukwati wa Mut`ah (ukwati wanthawi yochepa), komanso (adaletsanso) kudya abulu owetedwa (apakhomo).

4. Ndipo mkati-kati mwa kubwerera kwake kuchokera ku Khaybar adabwererako osamukira ku Habashah limodzi ndi Ja`far mwana wa *Abī Tālib* ndi *Abū Mūsā Al-Ash`arī* ndi anthu ake pambuyo pakuti adakhala zaka khumi.

5. Ndipo mchaka chimenechi adalandira Chisilamu atatu mwa akulu-akulu ankhondo a maquraysh omwe ndi: *Khālid ibn Al-Walīd*, *`Amr ibn Al-As* ndi *Uthman ibn Abī Talhah* (Allah awasangalire onsewa).

6. Ndipo mchaka chomwechi adatumiza Mtumiki (s.a.w) gulu laling'ono la nkhondo kuti likamenyane ndi mtundu wa *Banī Murrah*; lidawathira nkhondo ndipo lidapha ena mwa iwo ndipo lidagwira ena kukhala akapolo. Ndipo *Usāmah* (r.a) adathamangitsa munthu wina mwa iwo chomwecho Iye adanena Shahadah (mau a umboni wa chikhulupiriro), choncho *Usāmah* adayesa kuti (munthuyo) adanena zimenezo pofuna kudzipulumutsa basi, ndipo kenako adamufotokozera Mtumiki (s.a.w) chomwecho Iye adati: "Wamupha pambuyo pakuti adanena La ilaha illa Llah?!", ndipo adamulamura kuti amasule kapolo chifukwa chakuti adapha mwangozi.

7. Ndipo Iye (s.a.w) adakwatira ali ku Makkah *Maymunah bint Al-Hārith Al-Hilaliyyah* (yemwe adali) mkazi wawo wa bambo ake akulu *Hamzah* (r.a), ndipo Iye ndi otsiriza mwa akazi ake ndipo sadakumane naye mpaka pambuyo pa kutuluka ku Makkah.

MAFUNSO

Nchiani chomwe chidachitika kwa Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa kugonjetsa Khaybar? Kodi adakwatira ndani pambuyo pa kugonjetsa Khaybar? Kodi adaletsa chiani pamene Iye adali ku Khaybar? Ndani omwe adabwerako mkati mwa kubwerera kwake kuchokera ku Khaybar? Ndani omwe adalandira Chisilamu mchaka chachisanu ndi ziwiri? Kodi Mtumiki (s.a.w) adakwatira ndani ali ku Makkah?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHACHISANU NDI ZIWIRI (7)

Mchaka cha 7 kuchokera mu nsamuko idachitika nkhondo ya Khaybar; adaizungulira Mtumiki (s.a.w) masiku asanu ndi limodzi (6) ndipo kenako adampatsa mbendera ya nkhondo Ali Abi Talib (r.a) chomwecho adaigonjetsa.

Ndipo momwemo adachita mogwirizana wachiyanjano ndi Ayuda a Fadak pa kuteteza mwazi wawo ndipo adasiya chuma chawo. Ndipo adachitanso Mgwirizano wa chiyanjano ndi Ayuda a Tayma' pa kupereka nsonkho chomwecho adakhala mmizinda yawo mwamtendere.

Ndipo momwemo idachitika nkhondo ya Wadi al-Qura, ndipo momwemo adabwerera anthu osamukira ku Habashah.

Ndipo momwemo adatuluka Mtumiki (s.a.w) kupita ku Makkah. Ndipo momwemo adalandira Chisilamu Khalid mwana wa Walid ndi `Amr mwana wa Al-As ndi Uthman mwana wa Abi Talhah.

29. CHAKA CHACHISANU NDI ZITATU (8) KUCHOKERA MU NSAMUKO

Nkhondo zake – Malangizo a Mtumiki (s.a.w) kwa gulu la nkhondo la Mūtah – Kugonjetsedwa kwa Makkah

1. Mchaka cha 8 idachitika nkhondo ya *Mūtah* ndi nkhondo ya kugonjetsedwa kwa Makkah ndi nkhondo ya Hunayn ndi nkhondo ya *Tāif*.

2. Adawakonzekeretsa Mtumiki (s.a.w) kupita ku *Mūtah* anthu okwana zikwi zitatu (3,000) kukamenyana ndi omwe adapha nthumwi yake yopita kwa mtsogeleri wa Busrā.

3. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adawapatsa malangizo ena mwa iwo (nawa): (Mukawapeza kumeneko anthu ena omwe abindikira mmakachisi (kuchita mapemphero), chomwecho musakawapute, ndipo musakaphe mkazi, kapena mwana, ingakhalenso wachikulire otheratu, ndipo musakadule mtengo uliwonse ndipo musakagwetse chomanga chilichonse.

4. Chomwecho pamene iwo adafika ku *Mūtah* adapeza gulu la nkhondo lalikulu zedi lochokera ku Roma, chomwecho adamenyana nalo mpaka Zaid ibn Harithah (r.a) mtsogeleri wa nkhondo adaphedwa.

5. Chomwecho adatenga mbendera ndi Jafar mwana wa *Abi Talib* (r.a) ndipo adamenya nkhondo mpaka dzanja lake lamanja lidadulidwa, choncho adaitenga mbendera ija ku dzanja lake lamanzere ndipo linadulidwanso, chomwecho adaikumbatira kufikira adaphedwa. Chomwecho adaitenganso Abdullah mwana wa *Rawāhah* choncho adaphedwanso, choncho adaitenga (mbenderayo) mkango wanyonga *Khalid ibn Al-Walid* (r.a).

6. Chomwecho adamenyana nawo adani ndi luso lake lankhondo kumenya kwa mphamvu ndipo adapha mwa iwo gulu lalikulu kufikira adawapulumutsa Asilamu kuchokera kwa (adaniwo) ndipo adabwerera ku Madinah ndipo chomwecho Iye (Mtumiki s.a.w) adamutamandira Khalid (r.a).

MAFUNSO

Kodi ndi nkhondo ziti zomwe zidachitika mchaka cha 8? Tchulani chiwerengero cha asikali omwe adakonzekera Mtumiki (s.a.w) kukamenya nkhondo ya Mutah? Kodi Mtumiki (s.a.w) adawalangiza zotani? Kodi adapeza chiani pambuyo pa kufika kwawo ku Mutah? Kodi ndani yemwe adatenga mbendera ya nkhondo pambuyo pa Zaid mwana wa Harithah? Nchiani chomwe adachita Khalid pambuyo pakutenga mbendera?

30. NKHONDO YOGONJETSA (MAKKAH) PA 20 MU RAMADĀN

1. Chifukwa chake (chomwe chidachititsa nkhondo imenei) nchakuti maquraysh adaswa fundo imodzi mu fundo za pangano la mtendere la pa Hudaybiyah, ndipo iwo (maquraysh) adawathandizira omwe adachita nawo mgwirizano pa kuwamenya omwe adachita mgwirizano ndi Mtumiki (s.a.w).

2. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adayenda kupita kwa iwo pakati pa anthu zikwi khumi (10,000), ndipo adali atasala chomwecho adamasula ali mnjira.

3. Ndipo alonda a gulu la nkhondo adakumana ndi *Abū Sufyān* mnjira, yemwe adabwera kudzatolera nkhani za Asilamu.

4. Chomwecho adamugwira (adamumanga) ndikubwera naye kwa Mtumiki (s.a.w) choncho adalandira Chisilamu chomwecho Mtumiki (s.a.w) adamukhululukira.

5. Ndipo kenako Mtumiki (s.a.w) adatumiza *Khalid ibn Al-Walid* (r.a) kuti akailowe Makkah cha kumusi kwake, ndipo adamulamura kuti asamenyane ndi aliyense koma okhawo omwe angamenyane naye. Chomwecho mitundu ina (ya maquraysh) idamutsekereza kulowa (mu Makkah), chomwecho adamenyana nawo mpaka adawagonjetsa ndikulowa mu Makkah.

6. Koma akakhala Mtumiki (s.a.w) ndiye adalowela mbali ya kumtunda (kwa Makkah) popanda kumenyana kulikonse chifukwa chakuti palibe aliyense yemwe adamutsekereza kulowa.

MAFUNSO

Kodi nchiani chomwe chidayambitsa nkhondo ya Fat-h? Kodi adayenda ndi anthu angati Mtumiki (s.a.w) kukagonjetsa Makkah? Kodi alonda a gulu la nkhondo adakumana ndi chiani mnjira? Kodi adachita naye chiani? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani pambuyo pa zimenezo? Kodi adalowela mbali Mtumiki (s.a.w)?

31. LERO NDI TSIKU LA CHIFUNDO

1. Pamene Mtumiki (s.a.w) adafuna kulowa mu Makkah, adawawuza bamboo ake akulu Abbas (r.a) (kuti): "Muimitseni *Abū Sufyān* pamene akudutsa akavalo (a asilikali a nkhondo) kuti awone gulu la nkhondo la Asilamu".

2. Chomwecho mitundu yosiyana-siyana (ya ma Arabu achisilamu) inadutsa ndi mbendera (za nkhondo) uku *Abū Sufyān* akuona ndi maso namamufunsa Abbas (r.a) za maguluwo. Ndipo choncho pamene unadutsa mtundu wa ma Ansār – omwe mtsogeleri wawo adali *Sa`d ibn Ubādah* (r.a) – choncho iye adamutembenukira *Abū Sufyān* nati kwa iye: "**Lero ndi tsiku la nkhondo yadzaoneni; lero nyumba ya Ka`bah iloledwa (kuchitamo nkhondo)**". Chomwecho pamenepo *Abū Sufyān* adati: "**Bola likadakhala tsiku loteteza (abale ndi katundu)**".

3. Chomwecho pamene anadutsa Mtumiki (s.a.w) *Abū Sufyān* adati kwa Iye: "**Eti kodi walamura za kupha anthu ako?**". Iye adati: "Ayi (sindidalamure chomwecho)". Chomwecho iye adafotokoza mau a Sa`d, chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati: "**Wanama Sa`d (koma) lero ndi tsiku la chifundo, lero ivekedwa (nsalu) nyumba ya Ka`bah, lero Allah awalemekeza maquraysh**".

4. Ndipo kenako adatenga (adalanda) mbendera kwa *Sa`d* (r.a) ndikuipereka kwa mwana wake ndipo adalamura asikali ankhondo kuti asamenyane ndi aliyense koma amene angamenyane nawo basi.

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adati chiani kwa Abbas (r.a) pamene amalowa ku Makkah? Nchiani chomwe chidachitika pambuyo pa zimenezo? Nchiani chomwe adayankhula Abu Sufyan kwa Mtumiki (s..aw)? Nanga adamuyankha chiani? Nchiani chomwe adachita Mtumiki (s.a.w) pambuyo pa zimenezo?

32. KUKHULULUKA PANTHAWI YA MPHAMVU

1. Pamene Mtumiki (s.a.w) adalowa mu Makkah adawakhululukira maquraysh, ndipo oyitana ake adalengeza (kuti): "**Yemwe angalowe mu Masjid watetezeka, ndipo yemwe angalowe mnyumba ya Abi Sufyan watetezeka, ndipo yemwe angadzitsekere chitseko chake watetezeka**".

2. Ndipo adachotsera mu zimenezi anthu ena omwe adali opereka zedi masawutso kwa Asilamu, chomwecho ena adawapha ndipo ena adalandira Chisilamu chomwecho adawakhululukira.

3. Ndipo pamene adalowa mu Masjid adalamura za kugumula mafano omwe adali mu Ka`bah ndi mmbali mwake, ndipo adali mazana atatu ndi makumi asanu ndi limodzi (360), ndipo kenako adachita Takbeer ndikupemphera pa malo oyimapo Ibrahim (a.s), ndipo adamwa kuchokera mmadzi a Zamzam.

4. Ndipo kenako adakhala mMasjid uku anthu ali mmbali mwake akudikilira zomwe Iye awachite Amushrikuna a maquraysh amene adamusawutsa ndikumutululutsa mdziko lake ndipo adatsimikiza za kumupha ndikumuthira nkhondo.

5. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati kwa Iwo: "**E! Inu gulu la maquraysh! Kodi mukuganiza kuti ndichita chiani kwa Inu**?". Iwo adati: **"(Tikuganiza kuti uchita zabwino basi) (Ndiwe) m'bale wathu olemekezeka komanso mwana wa m'bale wathu olemekezeka**". Chomwecho Iye adati kwa Iwo: "**Pitani! Pakuti (nonseni) ndinu afulu**".

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani kwa maquraysh pambuyo pa kulowa mmakkah? Kodi adapatula aliyense wa iwo? Kodi adalamura chiani pamene adalowa mu Masjid? Adachita chiani pambuyo pa kumwa madzi a Zamzam? Nchiani chomwe adanena Mtumiki (s.a.w) kwa maquraysh?

33. KUPEREKA MALONJEZANO A KUGONJERA

1. Adayankhula Mtumiki (s.a.w) tsiku la kugonjetsa (kwa Makkah) mau omwe adafotokoza mkati mwake ambiri mwa malamuro a Chisilamu.

2. Ndipo kenako anthu adayamba kupereka malonjezano kwa Iye, ndipo ofunikira zedi omwe adalandira Chisilamu patsikulo (ndi) Mu`awiyah mwana wa Abi Sufyan ndi *Abū Quhāfah* atate ake a (Abubakr) *Siddīq*.

3. Ndipo adabwera kwa iye (Mtumiki s.a.w) munthu wina yemwe adali kunjenjemera chifukwa cha mantha (cha kumuopa), chomwecho Iye adati kwa iye: “Ika mtima wako pansi, pakuti Ine (sichina koma) ndine mwana wa mzimai omadya nyama yozonga”.

4. Ndipo pambuyo pa malonjezano a amuna, adamulonjeza iye akazi, ndipo adali kulonjeza (pa fundo zakuti); Iwo sadzamuphatikiza Allah ndi chinthu china, ndi kuti sadzaba ndikuchita chiwerewere, ndikuti sadzapha ana awo, ndikuti sadzanena bodza lamkunkhuniza lomwe akulipeka pakati pa manja awo ndi miyendo yawo, ndikuti sadzamunyozera Mtumiki (s.a.w) pa chinthu chabwino.

5. Ndipo kenako Mtumiki (s.a.w) adamulamura Bilal (r.a) kuti achite Adhan pamwamba pa Ka`bah, ndipo uku ndiko kuwonekera kwa Asilamu pamwamba pa nyumba yolemekezedwa.

6. Ndipo kenako adatumiza Mtumiki (s.a.w) magulu (ang’ono-ang’on ankhondo kuti akaphwanye mafano a mitundu (ya ma Arabu), chomwecho adaphwanyidwa `Uzzā ndi Suwā’ ndi Manāt.

7. Ndipo Mtumiki (s.a.w) anali kupungula Salah (popemphera maraka awiri-awiri mmalo mwa anai) munthawi ya kukhala kwake ku Makkah.

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adayankhula chiani tsiku la kugonjetsa Makkah? Kodi anthu adachita chiani pambuyo pa zimenezo? Ndani yemwe adamudzera panthawi imeneyo? Ndani omwe adamulonjeza pambuyo pa amuna? Nchiani chomwe Mtumiki (s.a.w) adamulamura Bilal? Nchiani chomwe adachita pambuyo pa zimenezo? Kodi adali kupemphera bwanji munthawi ya kukhala kwake ku Makkah?

34. NKHONDO YA HUNAYN

1. Idagwirizana mitundu (iwiri) ya *Thaqīf* ndi *Hawāzin* ndi mitundu ina za kuwathira nkhondo Asilamu asanawathire iwo nkhondo.

2. Chomwecho pamene Mtumiki (s.a.w) adamva zimenezo adatuluka kupita kwa iwo ali limodzi ndi anthu 10,000 kuchokera mwa anthu aku Madinah ndi anthu 2,000 mwa omwe adalandira Chisilamu tsiku la kugonjetsedwa kwa Makkah ndi 80 mwa Amushrikuna.

3. Chomwecho Asilamu adanyengeka ndi kuchuluka kwawo ndikuwadelera adani awo, kotero kuti ena a iwo adati: "**Sitingagonjetsedwe lero chifukwa cha kuchepa**".

4. Chomwecho pamene adafika ku chigwa cha Hunayn, adani adawalandira ndi mipaliro (yochuluka kukhala) ngati mvula, ndipo adali atabisala mmbali mwa mapiri a chigwacho ndi mmalo mothina mwake.

5. Chomwecho Asilamu adadzidzimutsidwa ndipo adagonja kuthawa, ndipo Mtumiki (s.a.w) adalimba limodzi ndi ochepa mwa ophunzira ake, ena mwa Iwo: Abubakr, Umar, Ali, Abbas, Abu Sufyan (yemwe ndi) mwana wa bambo ake akulu a Mtumiki (s.a.w).

6. Chomwecho adakuwa Abbas (r.a) ndi mau ake okweza (kuti): "**E! Inu eni malonjezano oyanjidwa!**". Chomwecho ma Ansar adayankha kuti: "**Tili pano tili pano**", ndipo adabwerera kwa Mtumiki (s.a.w).

7. Chomwecho Allah adatsitsa mtendere wake pa Mtumiki (s.a.w) ndi pa Asilamu ndipo adatsitsa asikali omwe iwo sadawaone, chomwecho adathira nkhondo pa adani awo ndipo adamenyana nawo mwamphamvu kufikira adawagonjetsa. Ndipo Asilamu adawatsatira uku akuwapha ndikuwagwira (ngati akapolo), ndipo adalandira Chisilamu ambiri mwa ma Amshrikuna omwe adali limodzi ndi Asilamu pa nkhondo imenei pamene adaona chisamaliro cha Allah pa Asilamu.

35. NKHONDO YA TAIF

1. Adayenda Mtumiki (s.a.w) kupita ku *Tāif* kukamenyana ndi omwe adathawira kumeneko mwa adani pa tsiku la Hunayn.

2. Choncho pamene adafika kumeneko adapeza kuti adani ali mmalinga awo ku Taif uku ali (atasungiratu) chakudya cha chaka chatunthu.

3. Ndipo pamene adawaona Asilamu adawalasa mwamphamvu ndi mipaliro kotero kuti adawavulaza ambiri mwa iwo ndipo adapha anthu khumi ndi awiri.

4. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawalasa ndi chida chotchedwa *Minjanīq* ndikuwazungulira masiku 18, ndipo kenako adawasiya mmalinga awo ndipo adati: "**E! Allah! Uwongoleni mtundu wa Thaqif ndipo mudze nawo (kwa ine) ali Asilamu**". Ndipo adabwerera ku Ji`irrānah kukagawa katundu wa ku nkhondo ya Hunayn.

5. Ndipo pambuyo pa misiku (angapo) adamudzera magulu a nthumwi za mtundu wa *Hawāzin* ali Asilamu, chomwecho adawapatsa ufulu wakusankha pakati pa kutenga akapolo kapena chuma, choncho iwo adasankha (kutenga) akapolo ndipo adasiya chuma.

MAFUNSO

Nchifukwa chiani adayenda Mtumiki (s.a.w) kupita ku Taif? Kodi adani adawapeza kuti pambuyo pa kulowa kwake? Kodi adani adachita chiani pamene adawaona Asilamu? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita nawo chiani? Ndani omwe adamudzera pamene Iye adali ku Ji`irrānah?

36. KUBWERERA KWA MTUMIKI (S.A.W) KUPITA KU MADINAH

1. Mtumiki (s.a.w) adakhala ku *Ji`irrānah* masiku 13 ndipo adachita Umrah kuchokera kumeneko ndipo adalowa mu Makkah chomwecho adachita *Tawāf* ndi kuwugwira mwala wakuda.

2. Ndipo kenako adabwerera ku Madinah mu usiku wake, ndipo mulingo wakusapezeka kwake kumeneko udali miyezi iwiri ndi masiku khumi ndi asanu ndi limodzi.

3. Ndipo pambuyo pa kubwerera kwake Iye (s.a.w) adatumiza magulu ankhondo ang'ono-ang'ono; kuti akaitanire mitundu ya ma Arabu ku Chisilamu.

4. Chomwecho adadza magulu a nthumwi kulowa mchipembedzo cha Allah magulu-gulu, ndipo Chisilamu chidafalikira mmaiko a ma Arabu.

5. Ndipo Asilamu adayamba kukonzekera kukafalitsa kuitanira ndi kuwawongola athu mmaiko (mmadera) ena.

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adakhala nyengo yotalika bwanji ku Ji`ranah? Kodi adabwerera liti ku Madinah? Nanga nyengo ya kusapezeka kwake ku Madinah idali yotalika bwanji? Adachita chiani pambuyo pa kubwelera kwake? Kodi pamenepo Asilamu adachita chiani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE CHAKA CHA 8 PAMBUYO PA NSAMUKO

Mchaka cha 8 idachitika nkhondo ya *Mūtah* ndipo adaphedwa mmenemo akulu-akulu a gulu la nkhondo (omwe ndi): Zaid mwana wa Harithah (r.a), ndi Ja`far mwana wa Abi Talib, ndi Abdullah mwana wa Rawāhah (r.a). choncho adaitenga mbendera ya nkhondo Khalid mwana wa Walid ndipo adapha mwa Aroma kupha kwa dzaoneni, ndipo adalipulumutsa gulu la nkhondo lachisilamu kwa Iwo (Aroma).

Ndipo mchaka chomwecho adagonjetsa Mtumiki (s.a.w) mzinda wa Makkah; chifukwa cha kuswa kwa maquraysh fundo imodzi mu fundo za pangano la Hudaybiyah. Mtumiki (s.a.w) adatuluka (kupita) kumeneko ndi anthu 10,000, ndipo Abu Sufyan adagwidwa ukapolo mnjira ndipo adalandira Chisilamu. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adakumana ndi bambo ake akulu Abbas (r.a) omwe adatuluka ku Makkah kukalandira Chisilamu, ndipo adabwerera naye limodzi. Adakumananso ndi Abu Sufyan mwana wa Al-Hārith, ndi Abdullah mwana wa Ummayyah chomwecho awiriwo adalandira Chisilamu.

Ndipo Mtumiki (s.a.w) adalowa mu Makkah mbali ya kumtunda kwake ndipo adamutumiza Khalid kuti alowere kumbali ya kumusi kwake, chomwecho anthu ena mwa maquraysh adamenyana naye koma Iye adawagonjetsa.

Ndipo Mtumiki (s.a.w) adawakhululukira maquraysh ndikuwapatsa chitetezo, ndipo adagumula mafano omwe adali mu Ka`bah ndi mmbali mwake. Ndipo amuna ndi akazi adamupatsa malonjezano awo ndipo ofunikira zedi omwe adalandira Chisilamu tsiku la kugonjetsedwa kwa Makkah ndi Abu Quhafah bambo ake a Abubakr Siddiq ndi Muawiyah mwana wa Abu Sufyan.

Ndipo mchaka chomwechi idachitika nkhondo ya Hunayn ndi Taif; adayenda Mtumiki (s.a.w) kupita ku Hunayn kukamenyana ndi mitundu iwiri ya Thaqif ndi Hawazin ali ndi asikali 20,000, chomwecho Asilamu adanyengeka ndi kuchuluka kwa chiwerengero chawo chomwecho adagonja kuthawa. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adalimba (osathawa) limodzi ndi gulu lina mwa ophunzira ake ndipo kenako Asilamu adabwerera (kupitiriza kumenya nkhondoyo) chomwecho Amushirkuna adagonja pambuyo pakuti adaphedwa mwa iwo anthu oposera 70 ndikugwidwa ukapolo ambiri mwa iwo ndi akazi awo ndi ana awo (ndikutengedwa) chuma chawo.

Ndipo kenako adayenda Mtumiki (s.a.w) kuwatsatira othawa mwa iwo chomwecho adawapeza atamanga malinga ku Taif , choncho adawazungulira kwa masiku 18, ndipo adaphedwa mwa Asilamu anthu 12. Ndipo kenako adabwerera Mtumiki (s.a.w) ku Ji`irranah chomwecho udadza kwa Iye mtundu wa *Hawāzin* kudzalandira Chisilamu, ndipo Iye adawalemekeza pa kuwabwezera akapolo (omwe anagwidwa mwa iwo) osati chuma.

Ndipo kenako adavala Ihrām ya Umrah ndikulowa ku Makkah ndipo kenako adabwerera ku Madinah mu usiku wake.

(37) CHAKA CHA 9 KUCHOKERA MU NSAMUKO

Nkhondo ya Tabūk

1. Mchaka cha 9 idachitika nkhondo ya Tabuk ndipo mudalibe kumenyana kulikonse.

2. Ndipo chomwe chidayambitsa chake nchakuti zidamufika Mtumiki (s.a.w) kuti Aroma asonkhana ku Sham (Syria) kuti akawathire nkhondo Asilamu mdziko lawo.

3. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adakonza gulu la nkhondo kuchokera mwa anthu ovutika omwe chiwerengero chawo chimakwana 30,000.

4. Ndipo adapempha chithandizo chake (chokonzekera nkhondoyi) kwa ochita bwino chomwecho iwo adayankha pempho la Mtumiki (s.a.w), ndipo yemwe adachulukitsa zedi kuthandiza anali Uthman mwana wa Affan (ndipo ameneyu ndiye kalembera oyamba mchisilamu).

5. Ndipo adamudzera Iye (s.a.w) anthu 7 mwa amphawi a ku Madinah kudzapempha kuti awapatse chokwera (popita ku nkhondoyi), chomwecho Iye adati kwa iwo: "**Sindikupeza choti (nkukupatsani) kuti mukwere popita ku nkhondo**". Chomwecho adabwerera maso awo atadzadza ndi misozi chifukwa cha kudandaula kuti sadapeze chokwerapo popita ku nkhondo. Chomwecho Allah adavumbulutsa pa nkhani ya anthu amenewa (mau akuti): "**Ndiponso (palibe tchimo) kwa amene akukudzera kuti uwatenge (kupita ku nkhondo) Iwe nunena: "Ndilibe choti ndikunyamulileni". Nabwerera maso awo akutuluka misozi chifukwa cha kudandaula posapeza zimene zingawathandize pa ulendowo**".

6. Ndipo kenako adayenda ndi gulu la nkhondolo mpaka adafika ku Tabuk, chomwecho sadapeze gulu la nkhondo lililonse ngati momwe zidamufikira.

MAFUNSO

Idachitika liti nkhondo ya Tabuk? Kodi gulu la nkhondo ya Tabuk adalikonza kuchokera mwa anthu otani? Tchulani chiwerengero chawo? Kodi chithandizo chake adachipempha kwa ndani? Ndani omwe adadza mu nthawi imenei? Adamupempha chiani?

38. KUTSALIRA KWA ANTHU A CHINYENGO

1. Pamene adakonzeka Mtumiki (s.a.w) za kutuluka (kunyamuka) anthu ena achinyengo (Amunafiquna) adati kwa anzawo: "**Musatuluke (kupita ku nkhondo) nthawi yotentha**". Chomwecho Allah adavumbulutsa pa nkhani ya iwo (mau akuti): **"….Nati kwa anzawo; "musapite (kunkhondo mnthawi yotenthayi". Awuze: "Moto wa Jahannam ngotentha kwambiri akadakhala akuzindikira**".

2. Chomwecho adatsalira mmbuyo Abdullah ibn Ubayy ndi ambiri mwa anthu achinyengo, (omwe) adatsika mau a Allah pa nkhani yokhudza iwo (onena kuti): "**Koma adakhala (popanda kupempha chilolezo kwa Mtumiki) amene amunamiza Allah ndi Mtumiki wake…**".

3. Ndipo adamupempha chilolezo Mtumiki (s.a.w) omwe adali ndi zifukwa zomveka mwa ma Arabu akumidzi ndi ena mwa anthu achinyengo chomwecho Mtumiki (s.a.w) adawapatsa chilolezo, choncho Allah adawasambula anthu achinyengowo ndi mau ake (onena kuti): "**Ukadakhala ulendo okafuna za mdziko zopepuka kuzipeza, ndi ulendo wofupika, ndithu akadakutsata Amunafiquna, koma ulendo wamavutowo wakhala wawutali kwa iwo. Ndipo iwo alumbira Allah ponena kuti: "Kukadakhala kofewa kwa ife tikadapita nanu". (Pa mau awa) akudziononga okha. Ndipo Allah akudziwa kuti iwo ngabodza**".

4. Ndipo Allah adamudzudzula Mtumiki (s.a.w) pa kuwapatsa chilolezo ndi mau ake (onena kuti): "**Allah wakukhululukira. Bwanji wawaloleza kutsalira? (Ukadayembekezera kufikira adziwike kwa iwe amene akunena zoona, ndikuti uwadziwe abodza. Sangakupemphe chilolezo (chotsara kunkhondo) amene akhulupirira Allah ndi tsiku lomaliza kuti asapite kukamenyera (chipembedzo cha Allah), ndi chuma chawo ndi matupi awo. Ndipo Allah akuwadziwa amene akuopa. Amakupempha chilolezo aja amene sakhulupirira Allah ndi tsiku la chimaliziro, ndipo mitima yawo yakaikira, ndipo iwo chifukwa cha kukaika kwawo akungotekeseka**".

5. Ndipo kenako Allah adawatsutsa pa kupereka chifukwa chawo ponena kuti: "**Akadafunadi kupita (ku nkhondo) akadakonzekera zokonzekera za ku nkhondo, koma Allah sadafune kuti iwo apiteko choncho adawatsekereza, ndipo kudanenedwa: "Khalani pamodzi ndi otsalira".**

6. Ndipo pofuna kuti Asilamu asataye mtima chifukwa cha kutsalira kwa Amunafiquna, chomwecho Allah adati: "**Ngati akadatuluka nanu pamodzi sakadakuonjezerani chilichonse koma chisokonezo ndi kuyenda mwa ukazitape pakati panu ndi cholinga chokufunirani chisokonezo, ndipo mwa inu alipo akuwamverera, ndipo Allah Ngodziwa za oipa. "Ndithudi akhala akukufunirani chisokonezo kuyambira kale, akusanthulira-santhulira zinthu (ndi cholinga choti athane nawe) kufikira chowonadi chadza ndikuonekera poyera lamulo la Allah Iwo asakufuna"**.

MAFUNSO

Nchiani chomwe chidachitika kwa ma Munafiqin pamene Mtumiki (s.a.w) adakonzeka za kutuluka kupita ku Tabuk? Ndani adatsalira mwa Iwo? Ndani omwe adapempha chilolezo chotsala mmbuyo kwa Mtumiki (s.a.w)? Kodi adawatsutsa a Munafiqun ndi chiani?

39. KUBWELERA KWA MTUMIKI KU MADINAH

1. Mtumiki (s.a.w) adakhala masiku angapo ku Tabuk omwe mkati mwake adamudzera Iye Yohane wamkulu wa mzinda wa *Aylah* ali limodzi ndi anthu a *Jarbā'a* ndi anthu a *Athrah* ndi anthu a mzinda wa *Mīnā'*, chomwecho (onsewo) adachita naye mgwirizano wa mtendere kuti adzipereka Jizyah (nsonkho) kwa Iye choncho Iye adawapatsa chitetezo.

2. Ndipo kenako adafunsa maganizo ophunzira ake za kuyenda kupita kumadera a kutsogolo kwa Tabuk.

3. Chomwecho Umar adati kwa Iye: "**Ngati mwalamulidwa za kupita kutsogolo pitani**". Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati: "**Ndikadakhala ndalamulidwa za kuyenda kupita chitsogolo sindikadafunsa maganizo**". Ndipo kenako adalamula za kubwerera ku Madinah.

4. Ndipo pamene adayandikira ku Madinah lidamudzera gulu la Amunafiquna kudzamupempha Iye kuti akawapempherere mu Msikiti wa *Dirār* (masautso).

5. Chomwecho adawafunsa za chifukwa cha kumangidwa kwake (Msikitiwo), choncho adalumbira Allah kuti; sitidafune china koma zabwino basi. Koma Allah akudziwa (akuchitira umboni) kuti iwo ndi abodza. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adalamura ophunzira ake za kuwugumula (Msikitiwo), chomwecho iwo adatero.

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adakhala nyengo yotalika bwanji ku Tabuk? Kodi adawafunsa maganizo ophunzira pa nkhani yanji? Adati chiani kwa Iye? Ndani omwe adadza pamene Iye adayandikira ku Madinah? Kodi adawafunsa za chiani?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHA 9 KUCHOKERA MU NSAMUKO

Mchaka cha 9 idachitika nkhondo ya Tabuk ndipo mudalibe kumenyana kulikonse. Mtumiki (s.a.w) adatuluka kupita kumeneko kukamenyana ndi magulu a Aroma ali limodzi ndi anthu 30,000 kuchokera mwa anthu ovutika (omwe) chithandizo chawo (ndi zofunikira zawo) adapereka ndi anthu ochita bwino. Ndipo omwe adali ndi zifukwa zomveka ndi gulu lina la Amunafiquna adamupempha chilolezo, choncho adawaloleza, tero Allah adawazazira Amunafiquna pa kupempha chilolezo kwawo.

Ndipo ku Tabuk adachita naye mgwirizano wa mtendere mkulu wa ku *Aylah* ndi ena omwe adali naye ndipo kenako adabwerera ku Madinah. Ndipo mkati mwa kubwerera kwake adalamura za kugumula Masjid ya masautso imene adaimanga Amunafiquna a kumadinah.

Ndipo pambuyo pa kufika kwake ku Madinah lidabwera kwa Iye gulu la nthumwi za ku *Thaqīf*. Ndipo mchaka chomwecho adamwalira Abdullah mwana wa Ubayy kapitawo wa Amunafiquna, ndipo adamwaliranso *Ummu Kulthūm* mwana wa Mtumiki (s.a.w).

40. CHAKA CHA KHUMI KUCHOKERA MU NSAMUKO

Nthumwi za ku Yemeni

1. Mchaka cha khumi adatumiza Mtumiki (s.a.w) Ali ibn Abi Talib ku mtundu wina wa anthu a ku Yemeni.

2. Ndipo adati kwa Iye: "**Yenda mpakana ukafike pa bwalo lawo ndipo ukawaitanire ku liwu lakuti "La ilaha illa Llahu". Chomwecho iwo akakayankha kuti inde, chomwecho ukawalamure za Salah ndipo usakaitanitse kwa iwo zina kusiya zimenezo, ndipo usakamenyane nawo mpakana atakumenya**".

3. Chomwecho pamene Ali (r.a) adafika kwa iwo adawaitanira ku Chisilamu chomwecho adakana, ndipo adawalasa Asilamu ndi mipaliro, chomwecho Asilamu adawathira nkhondo kufikira adawagonjetsa.

4. Chomwecho iye (Ali) adaletsa kuwathira nkhondo ndipo kenako adawafikira ndikuwaitanira ku Chisilamu chomwecho adayankha ndipo adati: "**Ife tili ndi udindo pa omwe ali mmbuyo mwathu mwa anthu athu, ndipo izi ndizo zopereka zathu (Zakat yathu) chomwecho tenga mmenemo choyenera cha Allah".** Choncho adachita zimenezo, ndipo kenako adabwerera kwa Mtumiki (s.a.w) chomwecho adamupeza Iye ali ku Makkah ku Hajj yotsanzikirana.

5. Ndipo kenako adatumiza Mtumiki (s.a.w) Muadh ibn Jabal (r.a) kupita ku mtunda kwa Yemen, ndi Abu Musa (r.a) kumusi kwake, ndipo adawalangiza Iye (s.a.w) ndi mau ake (onena kuti): "**Kafewetseni ndipo musakakitse (zinthu kumeneko)**".

6. Ndipo adati kwa Muadh (r.a): "**Ndithu iwe ukafika kwa anthu eni buku, chomwecho ukakawadzera ukawaitanire kuti akachitire umboni kuti palbe oyenera kupembedzedwa mwachoonadi koma Allah, ndikuti ndithu Muhammad (s.a.w) ndi mthenga wa Allah. Chomwecho ngati iwo akakuvomere pa zimenezo choncho ukawafotokozere kuti Allah wakakamiza pa iwo mapemphero asanu usana ndi usiku uliwonse. Chowecho ngati iwo akakuvomere pa zimenezo, ndiye ukawafotokozere kuti ndithu Allah wakakamiza pa iwo (kupereka) Sadaqah (chopereka cha ulere cha zakat) yomwe idzitengedwa kwa olemera awo ndikubwezedwa (kuperekedwa) kwa osauka awo. Chomwecho ngati iwo akakumvere pa zimenezo ndiye pewa ndikutalikira zolemekezeka za chuma chawo. Ndipo wopa pempho la munthu oponderezedwa, pakuti ndithu pakati pake ndi pakati pa Allah palibe chotchinga chilichonse**".

MAFUNSO

Kodi ndi nthawi iti yomwe Mtumiki (s.a.w) adatumiza Ali ku Yemeni? Kodi adati chiani kwa Iye? Kodi Ali adachita chiani atafika kwa Iwo? Kodi adachita chiani pamene adani adathawa kugonja? Nanga Mtumiki (s.a.w) adachita chiani pambuyo pa zimenezo? Adati chiani kwa Muadh?

41. HAJJ YAKUTSANZIKANA

1. Mchaka cha khumi adachita Hajj Mtumiki (s.a.w) Hajj yakutsanzika ndipo adali limodzi ndi anthu zikwi zisanu ndi zinai (90,000).

2. Ndipo imatchedwa kuti Hajj yakutsanzika: chifukwa chakuti Mtumiki (s.a.w) adawatsanzika Asilamu mmenemo, ndipo sadachite Hajj ina kupatula iyo.

3. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adachita Khutbah (ulaliki) tsiku la Arafah, Khutbah yotsanzika imene mkati mwake adafotokoza maziko a chipembedzo ndi nthambi zake.

4. Zina mwa izo ndi mau ake (s.a.w (akuti): "**Ndithu mwazi wanu ndi chuma chanu zili zoletsedwa pa inu kufikira mudzakumane ndi Mbuye wanu. Ndithu akazi anu ali nawo ufulu pa inu ndipo nanunso muli nawo ufulu pa iwo. Ndithu anthu okhulupirira ndi abale (kwa wina ndi nzake), ndipo sichololedwa kwa munthu aliyense chuma cha nzake koma kudzera mu kukondwa kwa mtima wake pa chumacho. Nonsenu ndi ochokera mwa Adam ndipo Adam ndi wochokera ku dothi. Ndithu wolemekezeka zedi wa inu ndi amene ali owopa zedi (Allah). Mu Arabu alibe ulemerero uliwonse pa osakhala wachiarabu koma kudzera mu kuopa Allah basi**".

5. Ndipo pa tsiku la Arafah idavumbulutsidwa Ayah (vesi) ya kukwaniritsidwa kwa chipembedzo (chachisilamu), yomwe ndi mau ake (Allah) Wapamwamba-mwamba (onena kuti): "**Lero ndakukwaniritsirani chipembedzo chanu ndipo ndakwaniritsa pa inu chisomo changa ndipo ndakusankhirani Chisilamu kukhala chipembedzo chanu**".

6. Ndipo pambuyo pakuti Mtumiki (s.a.w) adakwaniritsa mapemphero a Hajj adabwerera ku Madinah pambuyo pakuti adakhala ku Makkah masiku khumi.

MAFUNSO

Kodi Hajj yotsanzika idachitika chaka chanji? Nchifukwa chiani imatchedwa ndi dzina limeneli? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani tsiku la Arafah? Nchiani chomwe talowezapo kuchokera mu zomwe adayankhula? Nchiani chomwe chidavumbulutsidwa kwa Iye pa tsiku la Arafah? Kodi Mtumiki (s.a.w) adabwerera nthawi yanji ku Madinah? Nanga adakhala masiku angati ku Makkah atamaliza Hajj?

42. ZOCHITIKA-CHITIKA

1. Mchaka cha khumi ndi chomwe chili patsogolo pake (chaka cha 9) adachuluka magulu a nthumwi za ma Arabu (kudzalandira chipembedzo) ndipo anthu adalowa mchipembedzo cha Allah magulu magulu.

2. Chomwecho ena mwa magulu anthumwiwa (ndi); *Banu Hanifah* gulu la *Musaylamah* onama, ndipo onse adalandira Chisilamu kupatula *Musaylamah* onama pakuti iye adadziveka utumiki.

3. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adaziitanira nthumwi za Akhirisitu a ku *Najrān* ku Chisilamu chomwecho iwo adakana ndipo adati; "**Ife tidali Asilamu inu musadadze"**.

4. Chomwecho Mtumiki (s.a.w) adati kwa iwo; "**zikukuletsani kukhala Asilamu zinthu zitatu; Kupembedza kwanu mtanda, ndikudya nkhumba ndikunena kwanu kuti Allah ali ndi mwana**".

5. Chomwecho iwo adati; "**Ndani angafananenso ndi Yesu? Iye adalengedwa popanda bambo?**. Chomwecho Allah adavumbulutsa pankhani imeneyi (mau akuti); "**Ndithudi fanizo la Yesu kwa Mulungu lili ngati fanizo la Adam; adamulenga ndi dothi nanena kwa Iye kuti: "Khala munthu", ndipo adakhaladi"**. Ndipo pambuyo pa zimenezi adavomera kuti adzipereka Jizyah (nsonkho).

MAFUNSO

Ndinthawi iti yomwe magulu a nthumwi kupita Mtumiki (s.a.w) adachuluka? Ena mwa iwo ndi ndani? Ndi gulu liti la nthumwi lomwe Mtumiki (s.a.w) adaliitanira ku chipembedzo koma lidakana? Mtumiki (s.a.w) adati chiani kwa Iwo? Iwo adati chiani kwa Iye?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHA KHUMI KUCHOKERA KU NSAMUKO

Mchaka cha khumi adatumiza Mtumiki (s.a.w) Ali mwana wa Abi Talib kupita ku mtundu wina wa ku Yemeni, ndipo adamulamura kuti asawathire nkhondo mpaka ngati iwo atamuthira nkhondo. Chomwecho iwo adamuthira nkhondo chomwecho nayenso adawathira nkhondo mpaka adawagonjetsa. Ndipo kenako adawitanira (ku chisilamu) chomwecho adalandira Chisilamu.

Ndipo mchaka chomwechi adamutumiza Mu'ādh mwana wa Jabal ku dera la kumtunda la Yemeni, komanso Abu Musa Ash'arī kudera la kumusi kwake, ndipo adati kwa iwo: "**Kafewetseni ndipo musakalimbitse (zinthu kumeneko)".**

Ndipo mchaka chomwecho komanso chaka chapatsogolo pake, adachuluka magulu a nthumwi za ma Arabu. Ndipo Mtumiki (s.a.w) adachita Hajj ya kutsanzikana ndipo adachita Khutbah pa Arafah, momwe adawaphunzitsa anthu ambiri mwa maziko a chipembedzo ndi nthambi zake. Ndipo mchaka chomwecho adamwalira mwana wake Ibrahim (a.s).

43. KUKONZA GULU LA NKHONDO LA USAMAH (R.A)

1. Adakonza Mtumiki (s.a.w) asadamwalire gulu la asikali motsogozedwa ndi Usamah mwana wa Zaid (r.a) ndipo adamulamura kuti ayende mpaka ku *Ubnah* komwe adaphedwera bambo ake.

2. Ndipo mgulu la nkhondolo mudali ophunzira a Mtumiki akulu-akulu ochokera mwa ma Muhajirun ndi ma Ansar monga; Abubakr, Umar, Abu Ubaydah ndi Sa'd.

3. Chomwecho gulu lina lidatsutsa za utsogoleri wa Usamah pa akulu-akulu mwa ma Sahabah, chikhalirecho iye ndi mnyamata yemwe sadapitilire zaka 17 zakubadwa?

4. Chomwecho pamene Mtumiki (s.a.w) adadziwa zimenezo adakwiya mkwiyo wawukulu zedi ndipo adati kwa iwo: "**Tengani malangizo anga abwino pa iye, pakuti iye ndi mmodzi mwa abwino anu zedi**".

5. Koma ulendo wa gulu limeneli siudatheke mnthawi ya Mtumiki (s.a.w); chifukwa chakuti matenda adamuyambira mpakana adasiyana nalo dziko lapansi ndikupita ku dziko losatha.

MAFUNSO

Ndi gulu lanji la nkhondo lomwe adalikonza Mtumiki (sa..) atangotsala pang'ono kumwalira? Ndani adali mgulu limeneli mwa ophunzira a Mtumiki (sa.w)? Chidachitika nchiani pambuyo pake? Kodi Mtumiki (s.a.w) adachita chiani za kutsutsa kumeneku? Kodi gululi lidayenda mnthawi ya Mtumiiki (s.a.w)?

44. KUDWALA KWA MTUMIKI (S.A.W)

1. Adayamba matenda a Mutmiki (s.a.w) kumapeto kwa mwezi wa Safar mchaka cha khumi ndi chimodzi (11) kuchokera mu nsamuko.

2. Chomwecho adapitilira kudwala masiku khumi ndi atatu (omwe) mkati-kati mwake adali kumayenda (kumasuntha-suntha) mnyumba za akazi ake.

3. Koma pamene adakula matenda ake adawapempha (akazi akewo) chilolezo kuti adzikadwalira ku nyumba ya Aishah (r.a), chomwecha adamulola.

4. Ndipo pamene kutuluka kupita ku mapemphero kudamuvuta adati; "**Mulamuleni Abubakr awapempheretse anthu**". Chomwecho Iye (s.a.w) adamusankha iye Abubakr kukhala mlowa-malo wake akadali moyo.

5. Chomwecho pamene ma Ansar adamva za kukula kwa matenda ake, adasonkhana mu Masjid, chomwecho Abbas adamudziwitsa Mtumiki (s.a.w) za kusonkhana kwawo ndi kukhudzidwa kwawo.

6. Chomwecho adatuluka kwa iwo atamangilira nsalu mmutu mwake, akumakhwekhwereza pansi miyendo yake (kukanika kuyenda bwino-bwino), atatsamizira (pa mapewa) a *Ali* ndi *Fadl*, uku Abbas ali patsogolo pawo mpakana adakakhala pa chigawo cha chammusi zedi cha *mimmbar* (tsanja la mu Masjid). Chomwecho adamuyamika Allah ndi kumutamandira ndipo kenako adati: "**E! Inu anthu! Ndamva kuti mukuopa kumwalira kwa Mtumiki wanu. Kodi pali Mtumiki yemwe adakhala muyaya patsogolo panga mwa omwe Allah adawatumiza? Kotero kuti nanenso ndikhale muyaya? Imvani! Ndithudi Ine ndikukamuna ndi Mbuye wanga, ndipo ndthu nanunso mukakumana nane. Chomwecho ndikukulangizani za anthu osamuka oyambilira (kuwachitira) zabwino**".

MAFUNSO

Adayamba liti matenda a Mutmiki (s.a.w)? Adapitilira masiku angati kudwala? Kodi adachita chiani pamene matenda ake adakula? Adachita chiani pamene kudamuvuta kutuluka ku mapemphero? Kodi ma Ansar adachita chiani pamene adamva za kukula kwa matenda a Mtumiki (s.a.w)? Kodi Mtumiki (s.a.w) adatuluka kwa iwo?

45. KUMWALIRA KWA MTUMIKI (S.A.W)

1. Adamwalira Mtumiki (s.a.w) tsiku lolemba pa 12 mmwezi wa Raibiul Awwal mchaka cha 11 kuchokera mu nsamuko, ndipo zaka zake pa nthawi ya kumwalira kwake zidali 63, chomwecho Asilamu adadzidzimuka ndipo kusiyana naye kudawakulira.

2. Chomwecho Umar mwana wa Khattab adasolola lupanga lake ndipo adawopsyeza aliyense yemwe anganene kuti: Mtumiki (s.a.w) wamwalira. Ndipo adati: "**Ndithu Iye wangoitanidwa ngati momwe adaitaniridwa Musa choncho Iye anakhala kutali ndi anthu ake masiku makumi anai (40)**".

3. Ndipo Abubakr (panthawiyi) adali atachokapo, chomwecho pamene adabwera ndikuwuzidwa za nkhaniyi adalowa mnyumba ya Aishah (r.a) ndipo adavundukula nkhope ya Mtumiki (s.a.w) ndikuipsyopsyona nalira.

4. Ndipo kenako adatuluka kwa anthu nanena kuti: "**Imvani! Yemwe amapembedza Muhammad ndiye ndithu Muhammad wamwalira, koma yemwe amapembedza Allah ndiye ndithu Allah Ngwamoyo ndipo saafa**". Ndipo kenako adawerenga mau ake (Allah akuti): "**Ndithu Iwe udzafa, nawonso adzafa**". Ndi mau ake (a Allah onena kuti): "**Muhammad sali chinthu china koma Mtumiki chabe, patsogolo pake adamuka Atumiki ambiri. Kodi ngati atamwalira kapena kuphedwa mungabwererenso mmbuyo? Ndipo amene abwerere mmbuyo savutitsa Allah chilichonse, koma Allah adzalipira othokoza**".

5. Pamenepo Umar adati: "**Ngati kuti sindidawerengepo Ayah imenei**".

MAFUNSO

Adamwalira liti Mtumiki (s.a.w)? Kodi adali ndi zaka zingati panthawiyo? Kodi Umar mwana wa Khattab adachita chiani? Abubakr adali kuti panthawi ya kumwalira kwake? Kodi adachita chiani pambuyo pa zimenezo? Kodi Umar adati chiani pambuyo pa zimenezo?

46. KUYIKIDWA KWAKE MTUMIKI (S.A.W)

1. Adakhala Mtumiki (s.a.w) mnyumba yake (kuyambira) lolemba, ndi usiku wa lachiwiri ndi usana wake, ndi usiku wa lachitatu, kufikira asilamu adamaliza kukhazikitsa mtsogeleri (Khalifah) pa iwo.

2. Ndipo kenako adasambitsidwa ndi kuvekedwa sanda nsalu zitatu zomwe mudalibemo mkanjo ingakhalenso chilemba.

3. Ndipo kenako adaikidwa pa m'bedi mnyumba mwake, chomwecho asilamu adamupempherera (aliyense) payekha-payekha popanda imam (otsogolera); amuna kenako akazi kenako ana.

4. Ndipo kenako adaikidwa mchipinda cha Aishah (r.a) ndipo thumbila la manda ake lidanyamulidwa mulingo wa kutambasula chikhatho cha dzanja, ndipo (pathumbilapo) padawazidwa madzi.

5. Ndipo ndithu Mtumiki (s.a.w) adawasiira asilamu zinthu ziwiri, (zomwe) palibe chomwe chingawavute ngati iwo ali ogwiritsitsabe zimenezo.

6. (Choyamba ndicho) buku la Allah lomwe bodza silingalidzere patsogolo pake ingakhalenso kumbuyo kwake, (ndi chachiwiri) Hadith za Mtumiki (s.a.w) zomwe zidafotokozera chipembedzo ndipo zidafotokoza momveka bwino zolinga za Qur'an yolemekezeka.

MAFUNSO

Kodi Mtumiki (s.a.w) adakhala masiku angati mnyumba mwake atamwalira? Kodi adakonzedwa bwanji? Kodi adapempheredwa motani? Kodi adawasiira chiani asilamu pambuyo pa kumwalira kwake?

KUFOTOKOZA MWACHIDULE ZA CHAKA CHA KHUMI NDI CHIMODZI KUCHOKERA MU NSAMUKO

Mchaka cha 11 kuchokera mu nsamuko Mtumiki (s.a.w) adakonza gulu la nkhondo motsogozedwa ndi Usamah mwana wa Zaid (r.a), ndipo adamulamura kuti ayende kupita ku Ubnah. Ndipo (gululo) lisadanyamuke adayamba matenda ake Mtumiki (s.a.w) ndipo anadwalira mnyumba ya Aishah (r.a). Chomwecho pamene adakula matenda ake adamulamura Abubakr (r.a) kuti apempheretse anthu ndipo ma Ansar adasonkhana mmasjid, chomwecho Mtumiki (s.a.w) adatuluka kwa iwo ndipo adayankhula kwa iwo ulaliki wake omaliza, ndipo kenako adakumana ndi Mbuye wake tsiku lolemba pa 12 mmwezi wa Rabiul Awwal. Ndipo adakhalabe mnyumba yake (ali chimwalilireni) kufikira tsiku lachitatu, ndipo kenako adasambitsidwa ndi kuvekedwa sanda nsalu zitatu ndipo Asilamu adamupempherera nayikidwa mnyumba ya Aishah (r.a).

KUMALIZA: ANA AKE (MTUMIKI S.A.W)

1. Ana ake achimuna (s.a.w) alipo atatu; onsewo adamwalira patsogolo pake (Iye asadamwalire).

2. Iwo ndi: **Qāsim**[31]: anabadwa utumiki usadafike ndipo adakhala zaka ziwiri (zokha basi). Ndi **Ibrāhīm**: anabadwa mchaka cha 8 kuchokera mu nsamuko ndipo adakhala masiku 70 (okha basi). Ndi **Abdullah**[32]: anabadwa usadafike utumiki ndipo adamwalira ali wamng'ono.

3. Ndipo ana ake achikazi alipo anai: omwe ndi; **Zainab**[33]: Iye adachipeza chisilamu chomwecho adachilandira (chisilamucho). Ndi **Ruqayyah** ndi **Ummu Kulthūm** ndi **Fāṯimah**[34].

4. Ndipo onsewo adamwalira Iye asadamwalire kupatula Fāṯimah yekha basi, pakuti iye adakhala pambuyo pake miyezi isanu ndi umodzi (6).

MAFUNSO

Kodi ana ake amuna (s.a.w) alipo angati? Atchuleni maina awo? Nanga ana ake achikazi alipo angati? Atchuleni onse?

[31] Uyu ndi mwana oyamba kubadwa kwa Iye (s.a.w) usadafike utumiki.
[32] Amaitanidwanso ndi maina akuti Tayyib ndi Tāhir.
[33] Iye ndi wamkulu wa ane ake achikazi onse.
[34] Amaitanidwa kuti al-batūl (opatulika), chifukwa chakuti ndiwabwino zedi wa akazi onse a nthawi yake mu ulemelero ndi chipembedzo.

AKAZI AKE (MTUMIKI S.A.W)

1. Akazi ake Mtumiki (s.a.w) alipo 11; asanu ndi mmodzi mwa iwo ochokera mu mtundu wa quraysh (achiquraysh), ndipo anai ndi achiarabu wamba, pomwe mmodzi ndi ochokera mwa ana a Israyeli (wachiyuda).

2. Tsono achiquraysh ndi awa: **Khadījah** (r.a) mwana wa Khuwaylid; Iye (Mtumiki s.a.w) sadakwatire mkazi wina koma pambuyo pa kumwalira kwake basi. Ndi **Aishah** (r.a) mwana wa Abubakr Siddīq (r.a), ndi **Hafṣah** (r.a) mwana wa Umar (r.a), ndi **Ummu Habībah** (r.a) mwana wa Abī Sufyān (r.a), ndi **Ummu Salamah** (r.a) (yemwe ndi) **Hind** mwana wa Umayyah, ndi **Sawdah** (r.a) mwana wa Zam`ah.

3. Ndipo achiluya (wamba) ndi awa: **Zainab** mwana wa Jahsh (r.a), ndi **Maymunah** mwana wa Al-Hārith (r.a), ndi **Zainab** mwana wa Khuzaymah (r.a), ndi **Juwayriyyah** mwana wa Al-Hārith (r.a). Ndipo amene akuchokera mwa ana a Izirayeli ndi **Ṣafiyyah** (r.a) mwana wa Huyayy.

4. Ndipo mwa iwo (akazi) awiri adamwalira ali pansi pake (ali pa ukwati ndi Iye); (omwe ndi) Khadijah (r.a) ndi Zaynab (r.a) mwana wa Khuzaymah, ndipo Iye adamwalira ali ndi akazi 9 otsara.

5. Ndipo adzakazi ake alipo anai (ndipo iwo ndi awa): **Māriyah** wa chiqibṭiyyah (r.a), ndi **Rayhānah** al-Quradhiyyah (r.a), ndi wina mmodzi yemwe Zainab mwana wa Jahsh adampatsa Iye (ngati mphatso), ndi (wina) wachinai yemwe adamupeza kuchokera mu zopeza za kunkhondo.

MAFUNSO

Kodi akazi ake alipo angati? Ndani achiquraysh mwa iwo? Ndani achiarabu wamba mwa iwo? Ndani wachiyuda mwa iwo? Ndani omwe adamwalira mwa iwo ali pa banja ndi Iye?

AMALUME NDI AZAKHALI AKE (S.A.W): ANA A `ABDUL-MUTTALIB

1. Amalume ake (abale awo achimuna a bambo ake) alipo khumi, ndipo azakhali ake (omwe ndi abale awo achikazi a bambo ake) alipo asanu ndi mmodzi.

2. Amalume ake ndi; **Abū Tālib**[35], **Zubayr**, **Hamzah**, **Al-Muqawwam**, **bambo a Al-Fadl** omwe ndi Abbās[36], **Dirār**, **Hārith**, **Qutham**, **Abū Lahab**[37] ndi **Ghaydāq**.

3. Ndipo azakhali ake ndi awa; **Safiyyah**, **`Ātikah**, **Al-Bayda'u**, **Barrah**, **Umaymah**[38] ndi **Arwā**.

4. Ndipo mwa adzakhale ake palibe amene adalindira chisilamu koma Hamzah ndi `Abbās okha basi, (chimodzi-modzinso) mwa azakhali ake (palibe adalowa chisilamu) kupatula Safiyyah okha basi. Ndipo pali kusiyana maganizo pa nkhani ya (kulandira chisilamu kwa) `Ātikah ndi Arwā.

MAFUNSO

Kodi alipo angati abale awo a bambo ake achimuna ndi achikazi? Ndani omwe adalandira chisilamu mwa Iwo?

[35] Dzina lawo (leni-leni) ndi `Abdu Manāf.
[36] Abbās ndi mchimwene wawo wa Mtumiki (s.a.w) pa kuyamwira bele limodzi. Adamwalira mnthawi ya `Uthmān (r.a) ali ndi zaka 88.
[37] Dzina lawo ndi `Abdul-`Uzzā.
[38] Ndipo iwo anabadwa ngati mapasa ndi bambo ake a Mtumiki (s.a.w).

MAWONEKEDWE AKE NDI ZINA MWA KAKHALIDWE KAKE (S.A.W)

Mtumiki (s.a.w) adali okongola zedi mwa anthu onse mkabadwidwe kake; owala bwino nkhope yake, okongola bwino kamwa yake, mutu wake wawukulu bwino, otseguka ndi kuwala bwino chipumi chake, opyapyala bwino sidze zake, wachipumi chachikulu bwino, ochuluka zedi sidze za mmaso mwake, obiriwira bwino kampira kakuda ka mmaso mwake, ophanuka bwino zedi maso ake, wakamphuno kopyapyala ndi kotalika bwino zedi, otalika ndi kutambasuka bwino matsaya ake, wandevu zothinana bwino, olimba bwino zala za zikhatho za manja ake ndi za mapazi ake, olimba bwino mikono yake, otakasuka bwino mapewa ake, otambasuka bwino chidale chake. Ndipo sadali wamtali kapena wamfupi (koma wapakati-kati), otayana bwino tsitsi lake (lopeseka bwino), okoma zedi mau ake, ndipo mau ake amafika komwe mawu a ena sangafike. Kuseka kwake kudali kumwetulira basi, ndipo kuyenda kwake kunali kopendekera cha kutsogolo, kukhala ngati akutsetsereka pamalo otsika. Amati akatembenuka amatembenuka ndi thupi lake lonse osati ndi nkhope yokha basi ayi. Fungo labwino ndi lozuna lidali mbiri yake ngakhale asakhudze mafuta onunkhiritsa, ndipo sadayasamulepo ndipo sadageyepo ngakhale mpang’ono.

MAKHALIDWE AKE (MTUMIKI S.A.W)

Mtumiki (s.a.w) adali munthu okwanira zedi mchilengedwe ndipo adali okwanira zedi mmakhalidwe ndi dzina ndi nzeru. Adali okonda amphawi, wachifundo ndi anthu onse, wachisoni kwa iwo. Samakwiya koma chifukwa cha Allah basi, amakhululukira ndikunyalanyaza omwe amuchitira zoipa. Sadali otukwana kapena onyasa mmayankhulidwe (ndi zochitika zake), ndipo sadalinso otetembelera. Adali wamantha zedi ndi Allah, adali wanyonga (osaopa) ndi wamphamvu, opereka zedi ochita za ufulu. Wakuthwa zedi lilime lake, wozama zedi chiyankhulo chake; amawuyankhula mtundu uliwonse ndi lilime lawo (chinenero chawo), ndipo amayankhulitsana nawo ndi chiyankhulo chawo. Ophunzira ake samaimirira pamene Iye wafika chifukwa anali kudziwa (bwino) kuti Iye adali kudana nazo zoterozo.

ZOZIZWITSA ZAKE (S.A.W)

Zina mwa izo ndi: kugawikana pawiri kwa mwezi pamene maquraysh adamupempha zimenezo, ndi kutuluka (kubuka) kwa madzi kuchokera mzala zake pamene Iye adaika dzanja lake lolemekezeka mchiwiya chomwe mudali madzi ochepa.

Ndipo zinanso mwa izo ndi: kuchulukitsa chakudya chochepa.

Ndipo zinanso mwa izo ndi kuchiritsa odwala.

Ndipo chozizwitsa chake chachikulu zedi ndicho Qur'an; yomwe ma Arabu adalephera kubweretsa Sūrah yaifupi zedi yonga ngati iyo, (monga momwe akunenera Allah kuti): "**Nena, ngakhale atasonkhana anthu ndi ziwanda (mothandizana) kuti abwere ndi buku longa ili la Qur'an (mkayalidwe ka mau ndi matanthauzo ake) sangathe, ngakhale atathandizana wina ndi nzake**".

Chatha – (ndipo kutamandika konse ndi kwa Allah) – chidule cha mbiri ya wabwino zedi wa zolengedwa zonse (yemwe ndi Mtumiki s.a.w). Tikumpempha Allah kuti apereke mphamvu kwa muwerengi wa bukuli wa kugwiritsira ntchito chiphunzitso ndi chiwongoko cha Mtumiki (mtendere ndi madalitso a Allah akhale pa Iye ndi banja lake ndi ophunzira ake onse).